Mafunso ndi Mayankho pa Genesis

Tsopano, ngati wina ali nawo mafunso alionse amene iwo akufuna kuti awapereke muno, bwanji, ingowakankhirani iwo momwe muno kuno, muloleni mwana wina awabweretse iwo kapena chirichonse inu mukufuna kutero. Kapena, mwinamwake, ngati ife titi titsirize . . . Ine—ine ndiri nawo pafupi asanu ndi limodzi pa tsamba limodzi, ndipo tsopano pano, ndiye ife tiri nawo awiri cha uko.

2 Tsopano, ife—ife tiri kufuna kuti tipeze. Cholinga chimene ife tikuchitira ichi ndi kuti tifufuze chimene chiri pa malingaliro a anthu, zimene iwo ali kuziganiza. Mwaona? Ndizo zimene zimapanga mpingo wabwino, wamphamvu. Inu muyenera kuti muzikhala ndi—ndi nthawi, monga ngati inu mumayenerera kusasa akanzota achoke, inu mukudziwa, ndi chirichonse kuzichotsa zi—zinthu zonse pa njira kotero kuti inu mukhoza kumayenda bwinobwino. Kotero tsopano icho ndi cholinga ife timakhala ndi usiku wa mafunso kamodzi mwa kanthawi, ndi kuti tipeze.

3 Tsopano, ngati pali mafunso aliwonse amene . . . Tsopano, nthawi ino ine ndinakhala ngati kuchitsegulira icho, momasuka kwambiri. Ndipo ine ndinati . . . Tsopano, zinali mwakuti ine ndikanati, "Tsopano, ngati aliyense . . . basi chirichonse chokhudza kwa—kwa Lemba; yankho. Funsani ilo." (Zikomo inu, m'bale.) Ndipo ine ndinati, "Basi chirichonse chokhudza kwa Lemba; yankho." Mwaona, ndipo ife tikanati tiliyankhe ilo. Koma usikuuno ine ndinati . . .

4 Inu mukudziwa, ndiye iwo anabwera apo, iwo anati, "M'bale Bill," nandifunsa ine, "kodi inu mukuganiza ngati—ngati—ngati *Wakuti-ndi-wakuti* anachita chinthu *chakuti-chakuti,* kodi icho ndi Chikhristu?"

5 Chabwino, uko kuli ngati kukankhira kwina pa winawake. Koma ine ndinati, "Aloleni iwo akhale nazo izo usikuuno." Mwaona, izo zonse ziribwino. Kotero ife tikhoze kupeza ngati pali kukankhizirana kwina kulikonse kukuchitidwa.

6 O, ine—ine—ine ndikumverera bwino kwenikweni usikuuno. Ndimatchetcha udzu usana wonse, kotero ine ndikumverera bwino kwenikweni, panja mu dzuwa lotentha.

7 Ife tiri nao m—msonkhano ukudza posachedwa kwambiri tsopano, musati muyiwale. Ogasiti 23, pa Bwalo lalikulu mu Chicago, mpaka Septembala 5. Tikuyembekezera nthawi yopambana mwa Ambuye kumeneko. Ndipo izo zakhala

zikulengezedwa kulikonse tsopano, ndi mapepala osiyana onse alemba izo. Ndipo ife tiri kuyembekezera nthawi yopambana.

8 Tsopano, ine ndiri nao limodzi, awiri, atatu, anai, asanu, asanu ndi limodzi, ine ndikuganiza pa tsamba limodzi pano. Ndipo izo zonse zikunga ngati zokamba za chinthu chomwecho, kumbuyo mu—mu bukhu la Genesis.

9 Tsopano, choyamba ndi Genesis 1:26, kapena 1:26 mpaka 28, ndi pamene m—m munthuyu ndi. . . iwo anafunsa chomwe icho chikadakhala chiri. Chomwe—chomwe funso ili. . . Ine ndikutanthauza, anafunsa funsoli, mundikhululukire ine. Ndipo ife tikufuna kuti tiwerenge ilo poyamba. Tsopano, iwo anali atalilemba ilo pano. Ngati inu mukufuna kuti mulirondole ilo kwenikweni motsatira, izo zonse ziri bwino. Anati, "Mulungu analenga munthu, mwamuna ndi mkazi Iye anawalenga iwo." Mwaona? Ndiyeno potsatira iye ali ndi Genesis. . . kapena, bambowa kapena mayiwa, mmodzi, ali ndi Genesis 2.7," Iye anapanga munthu kuchokera ku fumbi lapansi." Apo ndi pamalo pena. Ine ndiwawerenga awo onse, chotero kuti ife tikhoze kuwatenga onse pamodzi pano kuti inu mukhoze kuona. Tsopano loyamba, gawo loyamba la ichi ndi, tsopano anati:

1. **"Mulungu analenga munthu, wamwamuna ndi wamkazi. Anamulenga munthu, wamwamuna ndi wamkazi."** Tsopano ndiyo, ine ndikuganiza, msonga yoyamba. **Tsopano mu Genesis 2:7 Ilo likuti, "Iye anapanga,"** (mzere pansi) "koma poyamba **Iye analenga."** Iye ali nawo ndiye. . . iye wayika mzere pansi pake. **"Ndipo Iye anapanga"** (mzere pansi) **"mwamuna kuchokera ku fumbi, ndipo anapumira mu mphuno zake." Ndi zina zotero. Tsopano, nchiani kusiyana kwake, kapena kuli pati kulumikizana mu Malemba a pamwambawa?**

10 Tsopano, ili ndi. . . Tsopano, ngati inu mwalilemba kale apo, Genesis 1:26 mpaka 28 ndi Genesis 2:7. Tsopano, ndi chinthu chokhudza zedi, ndipo ine—ine mwina sindingathe ayi. . . Ine ndangokhala ndi lingaliro langalanga la icho, kotero ine ndingolipereka ilo kwa inu momwe ine ndikumvera kuti izo ziri. Ndipo ngati inu mutsutsa, chabwino, izo nzabwinobe basi.

11 Ine ndikufuna kuti ndimuyamikire M'bale Neville pa mayankho abwino iye anapereka ku mafunso aja uko. Tsopano, iwo ndi abwino.

12 Tsopano, mu ili, Genesis 1:26, Mulungu anapanga munthu mu chifanizo cha Iyemwini. Ndipo ngati inu mukadati muzindikire, ife tizipeza izo kuti inu mukhoze kuziwerenga izo, ndi 26. . . Ngati inu mukufuna kuti muziwerenge motsatira ndi ife, ife tikadakhala wokonda kuti inu—kuti muchite izo, kundilondola ine bwino.

Ndipo Mulungu anati, Tiyeni ife tipange munthu mu chifanizo chathu, mwa mafanizidwe athu: ndipo aloleni

iwo akhale ndi ulamuliro pa nsomba za mnyanja,. . .pa mbalame *za mlengalenga,. . .pa zinyama za* padziko lapansi*. . .ndi pa chinthu chokwawa chirichonse chimene* chimakwawa *pa dziko lapansi.*

Kotero Mulungu analenga munthu mu chifanizo chake chomwe, mu chifanizo cha Mulungu Iye anamulenga iye; wamwamuna ndi wamkazi iye anawalenga iwo.

13 Tsopano, ndizo. . .Ine ndazimvapo izo zikukambidwa nthawi zambiri, ndipo kuzungulira dziko, zokambirana zimadzapo pa izo. Tsopano mu Genesis 2:7, penyani chimene Iye anachita apa. Chabwino, ndi Izi apa.

Ndipo. . .Mulungu anapanga munthu kuchokera *ku fumbi la mnthaka, ndipo anauzira mu mphuno zake mpweya wa moyo; ndipo* munthuyo *anakhala solo yamoyo.*

14 Tsopano, ndi mapangidwe a mtundu wanji. . .Wo—wofunsayu akufuna kuti afunse:

Ndi chilumikizo chanji chimene Genesis 1:26 uyu ali ndi Genesis 2:7? Mulungu analenga anthu awiri. **Ndi uti anali munthu, ndi amene. . .Ndi chilumikizano chanji chomwe ilo liri nacho? Chiyani. . .Kodi izo zikulumikizana bwanji mu Lembali?**

15 Chabwino, tsopano, ngati inu mutati muonetsetse mwatcheru tsopano, mu Genesis 1:26, tiyeni tipeze gawo loyambalo poyamba. Mulungu anati, "Tiyeni ife." Tsopano, "tiyeni ife," *ife* ndi. . .'Tiyeni ife tipange munthu mu chifanizo chathu chomwe." *Chathu*, ndithudi, ife tikuzindikira Iye akuyankhula kwa winawake, Iye anali kuyankhula kwa chamoyo china. "Tiyeni ife tipange munthu mu chifanizo chathu chomwe mofanana ndi ife, ndipo tiwalole iwo akhale ndi ulamuliro pa nyama za kuthengo."

16 Ngati inu mungazindikire, mu chilengedwe, chinthu choyamba chomwe chinalengedwa, ndithudi, kunali kuwala. Inu mukabwerabe pansi kudutsa mu chilengedwe, chinthu chomalizira chimene chinalengedwa chinali chiyani? Mwamuna. Ndipo mkazi anapangidwa pambuyo pa mwamuna. Chabwino, choyamba. . .Chinthu chotsirizira chimene chinalengedwa mwa kulenga kwa Mulungu, ndi mtundu wa munthu.

17 Koma pamene Mulungu anapanga munthu Wake woyambayo, ngati inu munaonetsetsa, Iye anamupanga iye mu chifanizidwe cha Iyemwini, iye anapangidwa mu chifano cha Mulungu. Ndipo Mulungu ndi chiyani? Tsopano, ngati ife tingathe kupeza chimene Mulungu ali, ife tikhoza kupeza mtundu wa munthu yemwe Iye anamupanga.

18 Tsopano mu Yohane Woyera, mutu wa 4, ndipo ine. . .inu muwerenge izi, Yesu akuyankhula kwa mkazi mu. . .ngati inu

mukufuna kuti mutsegule ku izo. Ine . . . posakhala ndi nthawi yokwanira, ine basi sindinawalembe iwo apa, ndingozitenga izo mwa chikumbumtima. Ndipo inu mukazifunefune izo tsopano, ngati ine ndingakhoze kuzipeza izo mofulumira ndithu. Tsopano tiyeni tiyambire cha pa mutu 4, ndi ndime ya 14:

> Ndipo *yense amene* amwako *madzi* awa *amene ine ndidzawapereka* kwa *iye sadzamva konse ludzu;* . . . ndi kukhala zitsime *za madzi zotumphukira mmwamba ku moyo wosatha.*
>
> *Mkaziyo* anati *kwa iye, Bwana, ndipatseni ine madzi awa, kuti ine . . . ndisamadzenso kuno kudzatunga.*
>
> *Yesu* anati . . . *Pita,* ndipo *kamuitane mwamuna wako,* . . .
>
> *Mkaziyo anayankha* . . .

19 Ine ndikukhulupirira ife tiyenera kuti tipite pamwamba pang'ono pa izo tsopano, kuti tizipeze, tipeze chimene—chimene ine ndikufuna inu kuti muchione pano. Mwina ayi, mwina ine ndikhoza kuchipeza icho popita pansi apa, ndi chomwe ine ndikufuna kuti ndichiwone. Mukuti chiani? Ndime ya 23 ndi ya 24. Chabwino

> *Inu mumapembedza* . . . (ndi pamenepa) . . . *Inu mumapembedza* ndipo inu *simumachidziwa icho: ife timadziwa chimene ife timachipembedza: pakuti chipulumutso ndi cha Ayuda.* (ndipo nkulondola, mwaona).
>
> *Koma ora likudza, . . . Koma ora likudza, ndipo tsopano liripo,* loti *opembedza owona* (Ayuda kapena Amitundu) *aziwapembedza Atate* mu *mzimu ndi mu choonadi: pakuti Atate amafuna oterewo kuti azimupembedza iye.*

20 Tsopano, ndime yotsatirayo ndi pamene ine ndikupafuna:

> *Mulungu ndi Mzimu: ndipo iwo amene ampembedza iye ayenera kumamupembedza iye mu mzimu ndi mu choonadi.*

21 Tsopano, ngati Mulungu analenga munthu mu chifanizo Chake Chomwe, ndi mu mafanizidwe Ake Omwe, ndi munthu wa mtundu wanji yemwe Iye anamulenga? Munthu wa mzimu. Tsopano, ngati inu muti muzindikire, Iye atapanga kulenga konse, ndi kulenga munthu wa mzimu, kuwerenga mosamalitsa kwa izi tsopano (kwa amene anafunsa funsoli) apeza izi, kuti Mulungu anapereka ulamuliro wa pa zinyama ndi nsomba ndi chirichonse kwa munthu. Koma, mu kumupanga kwake uko apo, Iye anamupanga munthu mu chifanizo Chake Chomwe kuti azitsogolera zinyama, azitsogolera zirombo za mthengo, mofanana monga mmene Mzimu Woyera umatsogolerera wokhulupirira lero. Mwaona?

22 Iye anali, mwa kuyankhula kwina, Adamu, mwamuna woyamba mu zolengedwa za pansi za Mulungu. Cholengedwa choyamba chinali Mulungu Mwiniwake; ndiye kuchokera mwa Mulungu kunadza Logos, amene anali Mwana wa Mulungu; ndiye kuchokera mu Logos, amene anali Mawu ("Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anapangidwa thupi ndipo anakhala pakati pathu."), Kuchokera mu Logos munadza m—munthu.

23 O, ine ndiri nacho chithunzi chokongola mu malingaliro anga tsopano, ngati inu mungakhoze kutenga kaulendo kakang'ono ndi ine. Ine ndikukhulupirira ine ndinayankhulapo pa icho kale, koma kuti ndichifikitse ichi pa malo pamene inu muti mukhale otsimikiza kuti muchione icho. Tsopano, tiyeni titenge kaulendo kakang'ono ndi kupita mmbuyo kwa kanthawi kakang'ono. Tsopano, musati muziganizira momwe kuliri kotentha tiyeni tifikitse malingaliro athu pa chomwecho chimene ife takhala tikuyankhula za icho ndi kumaganiza tsopano.

24 Tiyeni tipite mmbuyo zaka mamilioni zana kusanakhale nkomwe nyenyezi, mwezi, kapena chirirchonse mu dziko. Tsopano, kunali nthawi pamene kunalibiletu kalikonse kuno, icho chinangokhala chonse unthawizonse ndi Umuyaya. Ndipo unthawizonse wonsewo ndi Umuyayawo unali Mulungu, Iye anali kumeneko mu chiyambi.

25 Tsopano, tiyeni tipite cha kuno pamapeto pa chotchinga ichi ndi kuyang'ana uko nkumaona zinthu izi zikuchitika.

26 Tsopano, "Palibe munthu anawaonapo Atate pa nthawi iliyonse." Palibe munthu angakhoze kumuona Mulungu mu uthunthu wa thupi, chifukwa Mulungu sali mu maonekedwe a thupi, Mulungu ndi Mzimu. Mwaona? Chabwino. "Palibe munthu anawaonapo Atate, koma wobalidwa yekha wa Atate wamuonetsera Iye," ya 1 . . . Yohane, mwaona.

27 Tsopano, koma zindikirani tsopano, palibe chirichonse, pali danga lokha. Ndi kopanda kuwala, ndi kopanda mdima, ndi kopanda kanthu, uko kukungooneka kopanda kanthu. Koma mkati umo muli Wokhalapo wauzimu wamkulu, Yehova Mulungu, Amene anakwana mu danga lonse la malo onse pa nthawi zonse. Iye anali kuyambira kunthawizonse kuyambira kunthawizonse, Iye ali chiyambi cha chilengedwe. Uyo ndi Mulungu. Sungakhoze kuona kanthu, sungakhoze kumva kanthu, popanda kuyenda kwa atomu mmalere mopanda kanthu, kopanda ngakhale mpweya, kopanda kanthu, komabe Mulungu anali kumeneko. Uyo anali Mulungu. (Tsopano, tiyeni tiyang'ane kwa mphindi zochepa, ndipo patapita kanthawi . . .) Palibe munthu amene anaonapo Izo, tsopano, Awo ndi Atate. Uyo ndi Mulungu Atate.

28 Tsopano zindikirani. Ndiye patapita kanthawi ine ndikuyamba kuona Kuwala kwakung'ono kopatulika

kukuyamba kupangika, ngati kampira kakang'ono kapena kenakake, inu mukhoza kungokaona iko ndi maso auzimu.

29 Koma tayang'anani tsopano, pamene ife tiri kuyang'ana, mpingo wonse tsopano. Ife tiri kuimira pa chotchinga chachikulu kwambiri tikuyang'ana chimene Mulungu ali kuchita. Ndipo ife tifika mmbuyo momwe ku funso ili pano ndipo inu muona momwe Iye akuchibweretsera icho umo.

30 Tsopano, palibe, yemwe anamuonapo Mulungu. Ndipo tsopano, chinthu chotsatira ife tikuyamba kuchiona mwa maso a kupenya kwauzimu, ife tikuona Kuwala kwakung'ono koyera kukupangika kumeneko. Ndi chiani icho? Icho chinali kutchedwa, ndi owerenga Baibulo, "Logos" kapena "wodzozedwa," kapena "kudzoza," kapena m . . . monga ine ndimati ndinene, kuti g—gawo la Mulungu likuyamba kupangika kukhala chinachake kuti anthu okhalapo akanakhoza kukhala nalo lingaliro la mtundu winawake la chomwe chinali. Kanali kakang'ono, kotsika . . . Kuwala kwakung'ono, kukuyenda. Iye . . . Amenewo anali Mawu a Mulungu.

31 Tsopano, Mulungu anadzipatsa Yekha kubadwa kwa Mwana uyu amene analipo kusanakhale ngakhale atomu mu . . . kapena zopanga atomu. Icho chinali . . . mukuona, Yesu anati, "Ndilemekezeni Ine, Atate, ndi ulemerero umene Ife tinali nawo asanaikidwe maziko a dziko." Mwaona, kutali mmbuyo momwe umo.

32 Tsopano, mu Yohane Woyera 1, Iye anati, "Pa chiyambi kunali Mawu." Ndipo choyamba . . . "Ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anapangidwa thupi ndipo anakhala pakati pathu." Mulungu kudzifutukula Yekha, mpaka ku munthu wokhalapo. Tsopano penyani mmene Iye anachitira izo.

33 Tsopano, mmbuyo uko, ndiye, pamene kampira kakang'ono aka kakubwera. Tsopano, ife sitingakhoze kuona kanthu panobe, koma ndi maso auzimu chabe ife tikuona kuwala kutaima apo. Tsopano uyo ndi mwana wa Mulungu Logos. Tsopano, ine ndikukhoza kumuona Iye akusewera pamenepo monga mwana wamng'ono pa khomo la Atate ali ndi umuyaya wonse. Mwaona? Ndipo, tsopano, ndiye, mkati mwa mapangidwe Ake ongowalingalirawa Iye akuyamba kuganiza za zinthu zimene zikadati zidzakhalepo, ndipo ine ndikukhoza kumumva Iye akuti, "Siyani kukhale kuli kuwala."

34 Ndipo pamene Iye anatero, atomu inaphulika ndipo dzuwa linabwera nilikhalapo. Ilo linazungulira kwa zaka mamilioni mazana, kumapanga zidutswa ndi kumayaka ndi kumapanga monga izo ziriri lero; ziri kuyakabe, zikumanyosolabe maatomu. Ngati bomba la atomiki likanali lisiyidwe lokha chotero, kumangirizikana kwa atomiki kukanakhoza kulitenga . . . dziko ili likanakhala ngati dzuwa, kutaliko, kumangophulika ndi kupemerera. Ngati inu mukanakhoza kuima pamwamba pa

dziko lina ndi kumayang'ana kutali kwa ili ilo likanakhoza kumaoneka ngati dzuwa lina kumene maatomu anali kuyatsa dziko ili, ngati kulumikizana uko kukanakhoza kusiyidwa kokha, ndipo ilo nkuyamba kutembenuka, kugubuduzika monga chomwecho. Mamailosi mamilioni ndi mamilioni akufikirako malawi akulu awa, a—a—a kutentha kwa mabilioni a fahrenheit, komwe kukanamapita kuchokera ku dzuwa limenelo.

35 Tsopano, penyani izi tsopano. Zokongola! Tsopano, Iye anapanga dzuwa. Ndiyeno, chinthu choyamba inu mukudziwa, chibanthu chachikulu chinagwa kuchokera ku ilo, chinkalemera pafupi . . . basi pafupi ngati dziko ili, chinapita "Uphuu!" Ndiye Logos iyi pano tsopano, Mwana wa Mulungu akuchiyang'anira icho, Iye akuchilola icho kuti chigwe kwa zaka mamilioni zana ndipo Iye akuchiimitsa icho. Ndiye chimodzi china chikuulukira kwina, ndipo Iye akuchilola icho (kuulukira kwina) kugwa kwa zaka mamilioni, ndiye Iye akuimitsa icho. Tsopano ife taimirira, tikuziyang'ana izo zikudza nizikhalapo.

36 Tsopano, Iye ali nacho chinachake mu malingaliro Ake, ndipo kodi Iye akuchita chiani? Iye akulemba Baibulo Lake loyamba. Baibulo loyamba limene munthu ankayang'ana kwa ilo konse linali nyenyezi, zodiaki. Ndipo ilo ndi langwiro . . . basi . . . Ilo linalumikizana bwino ndi Baibulo ili pano. Ilo limayamba, choyamba cha zodiaki ndi namwali. Kodi kulondola uko? Chomalizira cha zodiaki ndi chiani? Leo, mkango. Ndiko kudza koyamba kwa Yesu, Iye anadza kupyolera mwa namwali; kachiwiri, Iye akubwera monga Mkango wa fuko la Yuda. Mwaona? Anazijambula izo zonse uko, m'badwo wa kansara, ndi chirichonse kutsika chodutsa. Tsopano, Iye anaika izo zonse mu mlengalenga nazikhazikitsa uko. Zidutswa zonse izi, zidutswa za dziko, kapena dzuwa, zikupachikika kuchokera apa.

37 Tsopano, pamene sayansi imapita kukafuna miyala iyo imene imagwa, izo sizimamutsutsa Mulungu, izo zimangotsimikizira icho kwa ine. Mwaona, izo zimangopangitsa izo kukhala chenicheni mochuluka. Tsopano, tsopano, zindikirani, miyala iyi yonse yapachikika kunja ukoyo yochokera ku dzuwa lotentha ilo, ndi kumapita kupyola mmalere, ndithudi, iyo yatolerana. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, izo inangoyambitsa phiri la madzi oundana.

38 Tsopano, ilo linali dziko ili likudza mu kukhalapo, chidutswa chokha chachikulu chakale cha khala chinagwa kuchokera kumeneko. Pansi mkati mwa icho tsopano, simuli kanthu koma chiphala choyaka chomadzitembenuza, mwathunthu, kuphulika kumabwera paliponse, ziphalazamoto. Ndipo sayansi imanena kuti—kuti dziko ili, chokhuthala cha pamwamba pa ilo, pamene ife timakhalapo, pali basi monga khungu la pa apulo. Ndipo onse . . . Tsopano, pali mamailosi zikwi makumi awiri mphambu zisanu kulizungulira (ilo liri pafupi mamailosi zikwi makumi

asanu ndi atatu) kukandapala. Ndipo ingoganizirani, cha mkati umo, ndi chiphala choyaka moto.

39 Ndipo magawo awiri pa atatu a dzikoli, bwinowo kuposera magawo awiri pa atatu a ilo, liri mu madzi; ndipo gawo limodzi pa atatu a ilo liri mu mtunda, pafupi gawo limodzi pa atatu. Ndipo chachinglono ichi, chokuta ichi chimene ife tiri kukhalapo, ipo pali podzaza ndi zophulika zoopsya, mpweya, petulo, mafuta, chirichonse. Kodi izo nzolondola? Ndipo magawo awiri pa atatu a ilo, bwinoko kuposera magawo awiri pa atatu a ilo, madzi. Kodi madzi ndi opangidwa ndi chiani? Magawo awiri a haidrojini ndi gawo limodzi la okosijeni, zophulika.

40 Muli magetsi okwanira mu chipinda chirichonse oti alekanitse kutentha ndi kuzizira, ndipo izo zingapange magetsi okwanira kuti ziphwasule chipinda. Inu mukhoza kuika maatomu okwanira mu mpira wa golfu kuti uphulitse New York kumuchotseratu pa nkhope ya dziko. Ndiyeno munthu atakhala pamwamba pa mphika wa gehena, amadzimenya yekha mu chifuwa ndi kumanyoza Mawu a Mulungu, ndi kumati, "Kulibe malo otero ngati gehena." (Ine ndiri nazo izo pansi apa pang'ono pokha, ndipo ife tipitirira kuti tifike ku izo, mwaona) Inu mukukhala pa mphika waukulu wa iyo tsiku lirilonse. Ndipo pamene inu mukadali kuno inu muli kukhala kumene pa iyo, ndipo gehena ili chapansi panupo basi.

41 Ndipo tsopano, zindikirani, koma tsopano pamene ichi chinapezeka koyamba, pamene Yesu . . . Tsopano penyesetsani kampira ka kuwala ako uko. Tsopano ine ndikukhoza kuona Iko kakuyenda kupita ku dziko ili ndi kukakhala pamwamba pa ilo ndi kuyamba kulisunthira ilo cha kuno pafupi ndi dzuwa. Ilo si china konse koma mpira waukulu wa madzi owundana. Ndipo pamene ilo likuyamba kusungunuka, ndiye mitsinje yaikulu kwambiri ya madzi osungunuka ikuyamba kung'amba modutsa ku mtunda uko mu maiko a kumpoto kumabwera mmusi. Ndipo pamene izo zinatero, zinang'ambira kunja Kansas ndi Texas ndi malo onse awo kumeneko, ndipo zinapita mpaka ku Chigwa cha Mexico. Ndipo chinthu choyambirira inu mukudziwa, chinthu chonsecho chinali chitaphimbidwa ndi madzi.

42 Ndiye, tsopano, ife tikufika mu Genesis 1, ife tikufika ku Baibulo tsopano, ndi kuchokera ku chithunzi chathu pa Baibulo. Genesis 1, "Dziko linali lopanda maonekedwe, ndi mopanda kanthu; ndipo madzi anali pamwamba pa nkhope yake mwakuya." Kodi izo nzolondola? "Ndipo Mzimu wa Mulungu unkayenda pamwamba pa madzi." Tsopano, Iye analekanitsa madzi, anabweretsapo zitunda, ndi dziko ndi zina zotero; nkuliumitsa ilo pambali. Zophuka ndi chirichonse, Iye anazipanga izo. Ndipo Iye anapanga mwezi. Ndipo anaika malire ake, a nyanja, kotero iyo sikanakhoza kupitirira.

43 Iye anali nazo zinthu zonse izo pamodzi, atazipanga . . . ? . . . Anapanga zinthu zina zonsezo, moyo wonse wazinyama, mbalame, njuchi, ankhwere, ndi chirichonse chomwe chinali, anaika zonse izo pano pa dziko. Ndiyeno Iye anafunsa funso ili tsopano. "Tiyeni ife" (Ndani? Atate ndi Mwana.) "tipange munthu mu chifanizo Chathu Chomwe."

44 Tsopano, ngati munthu akanati apangidwe chinachake chonga Kuwala kwakung'ono kopatulika kuja kutaliko, kapena chinachake changa iko, Iko sikukanati kuzioneka (chimene chiri Chokhalapo chauzimu). Iye anadzionetsera kapena anadzifunyulula Yekha mochulukira pang'ono, kuti apange utatu wa Iyemwini mwa Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Ndipo pano panali Mulungu, akudzifunyulula Yekha, tsopano pansipa mu "tiyeni ife tipange munthu," amene anali mwana Wake mphukira yochokera kwa Iye, "Munthu mu chifaniziro Chathu chomwe," Iye anali chokhalapo chauzimu. "Ndipo timulole iye akhale ndi ulamuliro pa zinyama za kuthengo, ndi zina zotero."

45 Tsopano, munthu ankatsogolera munthu . . . ankatsogolera zi—zinyama ndi chirichonse, basi monga Mzimu Woyera umatsogolerera wokhulupirira woona, weniweni lero. Liwu la Mulungu kunja uko . . . Liwu la munthu, kani, linkakhoza kuyankhula ndi kuti . . . kuitanira nyama mbali *iyi,* kuitanira nkhosa cha ku msipu uwu, kuitanira nsomba ku madzi *awa.* Mwaona, iye anali ndi ulamuliro, chirichonse chinkamumvera iye.

46 Tsopano, koma ndiye panalibe munthu woti azilima mu nthaka, Genesis 2, popanda munthu woti azilima mu nthaka. "Ndiyeno Mulungu anapanga munthu." (Genesis 2:7) "kuchokera ku fumbi la dziko." Tsopano Iye anatsatira . . . Iye anapanga munthu kuchokera ku fumbi la padziko, ndipo anayika Mzimu woposa chilengedwe uwu . . .

47 Tsopano, iye anali atagona apo. Ine ndikhoza kukhala ndi zithunzi zambiri za izo. Ine ndikukhoza kumuona Adamu ataima . . . Tiyeni ife tizitenge mwanjira *iyi,* kumuona iye ataimirira ngati mtengo. Mulungu anali atamupanga iye. Iye anali wakufa monga iye akanakhoza kukhala ali; zala zake zakumapazi, monga mizu, ziitazikika mu dothi. Ndipo Mulungu anati, "Siyani apo pakhale," kapena anapumira mpweya wamoyo mwa iye, ndipo iye analumpha, nakhala chomwe ali. Iye anali . . . Anapumira mpweya wamoyo mwa iye, iye anakhala solo yamoyo. Tsopano, ndipo iye anayamba kusunthira patsogolo, kumasuntha chitsogolo.

48 Ndiyeno Mulungu anatenga kuchokera mu mbali mwake gawo la iye, nthiti, ndipo anapanga mkazi. Tsopano, kodi Iye anautenga kuti mzimu, waukazi? Mwaona? Pamene Iye . . . Genesis 1:26, Iye anati, "Tiyeni ife tipange munthu mu chifanizo

cha ifeeni, mwa anthu omwe—mafanizidwe athu, anawalenga Iye iwo (munthu) wamwamuna ndi wamkazi." Iye anapanga mzimu wojintcha wa mwamuna; Iye anapanga mzimu wachikazi wanthete, waung'ono, wofewa kwa mkazi.

49 Ndipo pamene inu mumuona mkazi akumachita monga mwamuna, iye wachoka pa malo ake, inu mukuona, mwa kuyamba. Mwaona? Chabwino. Iye akuyenera . . . Ine ndikuganiza ndi chamanyazi kuti akazi ataya malo awo anthete, achikazi. Icho ndi chamanyazi. Ine ndikukuuzani inu, icho chiri. Ndicho . . . Inu mukudziwa, ine ndikuti ndinene ichi. Tsopano, ine sindikuyankhula za akazi inu pano. Koma, ndithudi, ngati icho chipweteka, icho chimangotero. Koma, penyani, ndiroleni ine ndikufunseni. Inu chinachake zinali mwakuti akazi anali achikazi kwambiri mpaka mwamuna akati aziyankhula kwa iwo ndipo iwo ankachita manyazi. Ha! Kodi manyazi nchiani, kwenikweni? Ine sindinazionepo izo kwa nthawi yaitali kwambiri ine sindikakhoza kudziwa ngakhale chomwe icho chikanakhala ngati mkazi wina akanamachita manyazi. Iwo alibiletu china cha zolemekezeka izo panonso, wonse uwo apo mzimu wabwino wachikazi. Iwo basi . . . Iwo akhoza . . . Iwo amavala zovala ngati mwamuna, kudula tsitsi lawo ngati mwamuna, kusuta ngati mwamuna, kumwa ngati mwamuna, kutukwana ngati mwamuna, kuvota ngati mwamuna, kugwira ntchito ngati mwamuna, chotero, kukhala wankhanza, wojintcha. O mayi! Izo zikusonyeza kumene inu mwafikako. Ndizo ndendende.

50 Zija zonga dona pang'onozi, inu simumaona iye kwambiri mochulukira, uyo ndi munthu wovuta kuti umupeze. Kodi izo si zolondola? Inde, icho ndi choonadi. Kotero mkazi si woyenera kuti aziimirira ndi kumachita ngati mwamuna, wamkulu ndi wojintcha, chifukwa iye ndi wanthete. Mulungu anamupanga iye mwanjira imeneyo. Ine ndikhoza kutsimikizira izo ndi Malemba. Inde, bwana. Izo ndi zolondola. Ndipo . . .

51 Koma, ndithudi, ife tikuchoka ku funso ili, koma ine sindikufuna kuti nditenge zambiri zochoka ku funso ili. Koma mukuona, apo ndi pamene Iye anapanga munthu Wake woyamba, anali mu chifaniziro Chake Chomwe.

52 Ndiyeno, Mulungu pasanakhale ngakhale nyenyezi, anadziwa kuti dziko ili likadadzakhalapo. Ndipo Iye anadziwa kuti ine ndikadadzakhala William Branham ndikulalikira uthenga kuchokera pa guwa ndipo inu mukanadzakhala *John Doe* mutakhala apo kumamvetsera kwa Iwo, dziko lisanayambe nkomwe. Aleluya!

53 Tsopano, apo ndi pamene anthu nthawizina, mu ma—makalvanisti ndi Amwachilamulo, amatenga zonse mosokonezeka. Mukuona? Iwo amati, "Chifukwa chiani kuti ena anakonzedweratu kuti adzataike?" Mulungu sali kulolera kuti

aliyense awonongeke. Iye sakufuna kuti aliyense awonongeke, komabe, pokhala Mulungu, Iye amadziwa pali ena amene sati awulandire Iwo. Mukuona? Mukuona, Iye ali nawo . . . Iye anayenera kuti awadziwe mapeto kuchokera kuchiyambi polinga kuti akhale Mulungu. Kodi Iye sakanatero?

54 Kotero Iye anadziwa kuti Iye akanati adzakhale ndi akazi ena, chotero Iye anangoupangiratu mzimu wao pomwepo. Baibulo linati Iye anatero, mu 1, Genesis 1:26, "Iye anamulenga iyeyo, mwamuna," mu maonekedwe oyambiriza, "wamwamuna ndi wamkazi." Ameni. Mwaona? Mu maonekedwe oyambiriza, Iye anamupanga mkazi ndi mwamuna iwo asanapangidwe nkomwe kuchokera ku fumbi lapansi.

55 Ndiyeno Mulungu anamupanga munthu, osati mu chifanizo Chake Chomwe. Thupi ili siliri mu chifanizo cha Mulungu, thupi ili liri mu chifanizo cha zirombo.

56 Kodi ine ndingakhoze kuvula chikhoto changa? Kukuyamba kutentha kutsogolo kuno. Ine ndiri ndi malaya ong'ambika, koma inu simutha kuzindikira izo. Mkazanga anandiuza ine kuti Jesse sanabwere ndi kudzatenga zochapa, chotero . . . Koma, penyani, ife tiri pa phunziro pano tsopano limene likutanthauza zochuluka kuposa malaya ong'ambika pa guwa. Si choncho? Ilo likutanthauza Moyo Wamuyaya.

57 Tsopano, zindikirani munthu. Mulungu ankadziwa pa chiyambi kuti Iye amati adzakhale nawo amuna ndi akazi, ndipo Iye ankadziwa kuti Mpulumutsi akanati adzakhalepo kuno, ndipo Iye akanati adzamubweretse Yesu, ndipo akanati adzapachikidwe. Ndipo Yesu anawauza ophunzira, pamene Iye anali pa dziko pano, kuti Iye "anawadziwa iwo ngakhale asanaikidwe maziko a dziko," dziko lisanadze nkomwe pa kukhalapo.

58 Ndipo Mulungu anati, ndiponso, kapena Paulo poyankhula, mu Agalatiya, ananena kuti, "Iye anatikonzeratu ife ndipo anatiitana ife mwa Iye lisanapangidwe nkomwe dziko." Taganizani za izo! Mulungu uyo . . . Wina aliyense akadakonda kuti amve chimene Lemba limanena pa izo, kwezani manja anu. Izo zikuyendera limodzi kumene ndi funsoli. Pezani ndi ine mu Agalatiya, mutu wa 1. Taonani apa. Ine sindikutanthauza mu Agalatiya, Ine ndikutanthauza Aefeso. Mvetserani mwatcheru tsopano chimene Mulungu ananena, Aefeso 1:

> *Paulo, mtumwi wa Yesu Khristu mwa chifuniro cha Mulungu, kwa oyera omwe ali ku Efeso, ndi kwa okhulupirika mwa* Yesu Khristu.
>
> *Chisomo* chikhale *kwa inu, ndi mtendere, kuchokera kwa Mulungu Atate, ndi kuchokera kwa Ambuye Yesu Khristu.*
>
> *Adalitsidwe Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Khristu, amene watidalitsa ife ndi madalitso onse*

auzimu mu malo ammwambamwamba mwa Khristu Yesu.

59 Tsopano, ndi ichi apa, zindikirani:

Malingana ndi momwe iye anatisankhira ife mwa iye asanaikidwe maziko a dziko, . . . (fyuu!)

60 Izo ndi zabwino kwambiri. Si choncho? Izo sizabwino kwambiri, izo ndi zabwino kwenikweni! Pasanakhale maziko a dziko, Mulungu anamudziwa Orman Neville ndipo anadziwa kuti iye akadamadzalalikira Uthenga. Kodi izo sizodabwitsa? "Anatisankha . . ." Bwanji Iye ndi membala wa Mpingo, ndipo Mulungu anadziwa Iye akanati adzakhale ndi Mpingo umenewo. Ndipo iye anati, Paulo akuyankhula kwa mpingo waku Efeso, anati, "Iye anatisankha ife mwa Iye." Tsopano, ife tonse ndife ziwalo za Thupi la Khristu. Izo ndi zolondola? Ndipo Mulungu, lisanakhalepo dziko nkomwe, anakusankhani inu ndi ine mwa Iye lisanapangidwe dziko nkomwe. Fyuu! Mai! Kodi izo si zodabwitsa?

61 Tsopano, munthu woyamba, tsopano, Iye anamupanga munthu woyamba mwa chifanizo *Chake*, ndipo ife tikubwereranso ku chifanizo chimenecho izo ndi zolondola, ku chifanizo chathu choyamba cholengedwa.

62 Pamene Mulungu anandilenga ine, William Branham, ine ndinalipo asanaikidwe maziko a dziko, Iye anapanga chomwe ndiri, mzimu wanga. Ine sindinali kudziwa za chirichonse momwe ine ndikudziwira, koma . . . ine ndinalipo kumeneko. O, ine—ine sindikukhulupirira kuti inu mukuchimvetsa ichi. Koma tsopano, miniti yokha, Yesu anawauza ophunzira kuti Iye "anawadziwa iwo asanaikidwe maziko a dziko" ndipo Paulo ananena pano kuti, "Iye anatisankha ife mwa Iye dziko lisanayambe." Tsopano, panali gawo lina la ine, Orman Neville, ndi ena nonse a inu muno, amene muli mwa Khristu Yesu dziko lisanayambe nkomwe. Ndipo apa pali mwa kugawa kwanga pa izo. Ine ndikuganiza kuti anthu lero amene ali ogwidwa ndi Mzimu umenewu, kapena mzimuwo, gawo la zomwe ziri zaungelo izi, mizimu imene imazungulira kuchokera kwa Mulungu, imene siinagwe nawo mu chiyambi ndipo inakaniratu bodza la Mdierekezi Kumwamba.

63 Ndipo magawo awiri pa atatu a dziko ali mu utchimo, ndi mochuluka kuposa apo, amene magawo awiri pa atatu a angelo anakankhidwira kunja. Ndipo mizimu ya ziwanda imeneyo imadza mwa anthu, ndi kumakhala mu matupi awo. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Izo ndi ziwanda zimene nthawi ina . . . izo nthawiina zinalipo ndipo izo zimadza mwa anthu ndi kuwapatsa iwo khalidwe. Yesu anatulutsa zisanu ndi ziwiri za izo kuchokera mwa Mariya wa Magadala. Kunyada, kudzitukumula, (anthu aakulu, inu mukuona),

osayera, chinyanso, kulaula, matukutuku, ndeu. Zinthu zonse izi, mwaona.

64 Iyo inali mizimu imene inapangidwa kumbuyo uko, pamene Mulungu anayamba kumupanga munthu mwa chifanizo Chake Chomwe. Analenga zomwe ziri zoposa zachilengedwe, mizimu imeneyo.

65 Ndiyeno Iye anamuika munthu mu fumbi lapadziko, amene anali munthu woyamba, Adamu. Ndipo munthu ameneyo anapangidwa mu chifanizo, munthu waumunthu uyu apa, ndi wopangidwa motengera chifanizo cha chinyama. Matupi aumunthu awa ndi opangidwa mu chifanizo cha zinyama.

66 Ife tiri ndi dzanja longa ngati la nkhwere, ndi—ndipo tiri ndi phazi longa la chimbalangondo. Mukatenge kamwana ka chimbalangondo kakang'ono, kasendeni iko motsitsa konse, kokani chikopacho kuchichotsa pa iye ndipo kakaikeni moimiritsa pambali ndi kamtsikana kakang'ono kakhanda ndipo penyani kusiyana kwake. Hu! M'bale, inu zedi muyenera kuchita kuyang'ana mwapafupi. Kumimba konseku, kapangidwe kake, ndi pafupi zofanana, momwe izo zinapangidwira ndi kaumbidwe ka iyo ndi chirichonse ndendende basi. Izo ziri mu chifanizo cha moyo wa zinyama chifukwa iye anapangidwa chinachake cha pa dongosolo la chinyama, chifukwa iyo inali ntchito yake kuti azitsogolera zinyama.

67 Ndipo inu mukautenga Mzimu Woyera nkuuchotsa pa munthu, iye ndi wotsika kuposa chinyama, iye ndi woipa kuposa chinyama. Icho ndi chinthu cholimba kuti uchinene. Koma inu mumutenge munthu amene ali wosatembenuka mu malingaliro ake, wopanda Mzimu Woyera woti uzitsogolera maganizo ake, ndi—ndi zinthu monga choncho, iye akhoza kutaya khanda kulichotsa mmanja mwa mayi ndi kumuchita zoipa chifukwa cha chilakolako cha uchirombo. Izo ziri ndendende.

68 Ndipo mkazi amene si wabwino. Inu mukatenga nkhumba yaikulu yaikazi kapena galu wamkulu, ife tamupatsa kale iye maina onse amitundu pa izo. . . Koma makhalidwe ake ndi a tiagalu take basi, ndipo nkhumba a tinkhumba take, koma mkazi woipa wa mbiri yosakhala yabwino wangokhala ali basi ngati. . . zauve nthawizonse. Uko nkulondola. Chotero kumbukirani kuti inu ndinu. . . wopanda Khristu, makhalidwe anu ali. . . akhoza kugwera pansi mpaka pansi pa garu. Ndiko kulondola.

69 Garu samasowa kuti azivala zovala kuti adziphimbe yekha, palibe chinyama chinanso. Anali munthu yemwe anagwa, osati moyo wa chinyama. Koma, moyo wa chinyama pokhala pansi pa munthu (moyo wa umunthu), unali womvera kwa iwo, chifukwa munthu anali namlondola wake ndi mtsogoleri

wake wamkulu. Ndipo chirombo chirichonse cha kuthengo chimamuopa munthu.

70 Winawake anali kundifunsa ine, nthawiina, za kusaka, "Kodi inu mumakhala owopa izo?" Bwanji, chinyama chirichonse chinalengedwa konse chimaopa munthu, chifukwa izo ziyenera kukhala motero kuchokera pa chiyambi mpaka kutaliko. Mwaona? Ndithudi. Inu mumathawa ndipo iye akuthamangirani pambuyo panu, izo ndi zolondola, koma, garu, kapena chirichonse chomwe mukufuna chitero. Chabwino.

71 Koma tsopano, zindikirani tsopano, munthu uyo pamene anabwera pansi pano, . . . Tsopano onani, pano . . . Inu mukuti, "Tsopano, nanga bwanji za izo tsopano, M'bale Branham?"

72 Tsopano, pano inu mupeza Mulungu mwa ndendende basi, ndipo pakati pa umodzi ndi utatu inu mudzapeza chinthucho mwa ndendende basi pomwe pano. Tsopano penyani! Pamene Mulungu anatsika, anadzifutukula Yekha, anadzifutukula yekha pansi mpaka Iye amadza pansi kwa munthu uyu. Tsopano, munthu anachimwa osati mu mzimu wake, koma mu thupi lake, kukhumbira chilakolako. Ndiye pamene iye anachimwa, iye anadzilekanitsa yekha kwa womupanga Wake. Ndiyeno Mulungu, Logos, Mlengi yemwe wa iye, anadza pansi ndipo anapangidwa mu chifanizo cha munthu. Munthu anapangidwa mu chifanizo cha Mulungu, ndiyeno iye anapangidwa mu chifanizo cha chirombo, ndipo iye anagwa. Ndipo Mulungu anadza pansi mu chifanizo cha Munthu, mwa Munthu Khristu Yesu, kuti adzamve zowawa. Mulungu sakanakhoza kumva zowawa mu Mzimu. Iye akanakhoza bwanji kumva zowawa zathupi mu Mzimu? Iye sakanakhoza kuchita icho. Kotero Mulungu anadzifutukula Yekha ndipo anapangidwa mwa chifanizo cha munthu, kuti amuombole munthu amene anali atataika. Mwaona?

73 Ndiyeno Mulungu anamva zowawa mu thupi. 1 Timoteo 3:16, "Mopanda kutsutsa," Ndiwo mkangano, "chachikulu ndi chinsinsi cha umulungu. Pakuti Mulungu anaonekera mu thupi, anaonedwa ndi angelo, analalikidwapo, kwa Ami- . . . ndipo anakhulupiriridwa, ndipo analandiridwa kumwamba ku dzanja lamanja la Atate." Kodi izo nzolondola? Mulungu Mwiniwake anadza pansi ndipo ankakhala mu thupi laumunthu ndipo anavutika nao mayesero." Mulungu anali mwa Khristu, akuliyanjanitsa dziko kwa Iyeyekha." Mukuona chomwe chikondi chiri? Chikondi cha Mulungu!

74 Tsopano, tsopano, ine ndikuganiza izo zikanakhoza kumutenga uyo *mwamuna* ndi *mkazi*. Tsopano, mkazi ali . . . Ndisiyeni ine ndichibweretse ichi mkati mwabwino tsopano, kuti inu mukhoze kuchiona icho, mwaona. Mkazi ndi womvera kwa mwamuna wake. Ndipo Baibulo linanena kuti "Mwamuna azilamulira pa mkazi wake." Koma momwe iwo azisinthira

izo! Mkazi akulamula pa mwamuna, "Tsopano, iwe ukhale ku nyumba, Yohane! Iwe suli kupita!" Ndipo izo zimakhazikitsa icho, "Inde, wokondedwa wanga." Mwaona?

75 Koma ndisiyeni ine ndikuuzeni inu chinachake, bambo. Inu mudzayenera kudzayankhira pa mkazi wanu, koma mkazi wanu sati adzakuyankhireni konse inu. Inu ndinu mutu wa mkazi, ndipo Mulungu ndi mutu wa mwamuna. Chotero Iye anati, "Msiyeni mwamuna azimeta tsitsi lake chifukwa cha Khristu. Ndipo msiyeni mkazi azikhala nalo tsitsi lake, pakuti ngati iye adula tsitsi lake iye amamunyozetsa mwamuna wake." Mwaona? Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza pa chimene Lemba likunena?

76 Ine ndinali nalo lina lotentha pa izo, uko tsiku lina ku Shreveport. Iwo anali kuyankhula za akazi, ndi ngati akazi ayenera kumavala tsitsi lalitali. Ndipo ine ndinati, "Mkazi amene amadula tsitsi lake, mwamuna wake ali ndi ufulu, ndi ufulu wa Baibulo kuti amusiye iye." Uko ndi zolondola. Ndi zomwe Baibulo limanena. Izo ndi zolondola ndendende. O, mai! Akazi a Mzimu Woyera atakhala pamenepo, monga mmene iwo anaphunzitsidwira basi, ndizo zonse. Mwaona? Basi, ndimo anatelelekera mosasamala.

77 Iye anati, "Tsopano, ngati iwo akanati alidule ilo, ngati pakanakhala chinachake cholakwika iwo anayenera azilidula tsitsi lawo," anati, "akanalola iye atenge lumo ndi kulimeta ilo lonse kulichotseratu," ndi kulipangitsa tsitsi lake kuoneka bwino kwenikweni, mpaka ilo lita theratu pa mutu wakepo. Uko nkulondola. Izo ndi zimene Lemba linanena. Ndipo Ilo limati, "Ngati iye adula tsitsi lake, iye amamunyozetsa mwamuna wake. Ndipo mkazi amene ali wopanda ulemu ali nawo ufulu mwalamulo kuti achotsedwe ndi kusiyidwa." Koma, iye sangakhoze kukwatiranso ayi, tsopano. Koma iye—koma iye akhoza kumuchotsa iye mwa chilekano. Izo ndi zolondola. Ilo ndi lemba. O m'bale, chomwe ife tikusowa ndi mausiku amafunso! Ndiko kulondola. Uyo ndi 1 Akorinto, mutu wa 14, ngati inu mukufuna kuti muziwerenge izo. Chabwino. Tsopano, izo—izo . . . Tsopano, mkazi uyu . . .

78 Mulungu—Mulungu analenga munthu, wamwamuna ndi wamkazi. Mukuona chimene Iye anachita? Iye anamupanga munthu. Iye anapanga . . . Tsopano, ilo ndi funso loyamba mwaona, "Iye anawalenga iwo," ndi zina zotero, Genesis 1:26. Genesis 2:7. "Iye anawapanga iwo kuchokera ku fumbi la padziko ndipo anapumira mu mphuno zake."

Kusiyana kwake ndi chiyani, kapena—kapena chiri pati chilumikizo ichi mu Lemba lapamwambali? Ndi chilumikizano chanji chimene munthu Woyambayu ali nacho ndi munthu wachiwiriyu?

79 Munthu woyambayo ndi munthu wachiwiriyu atapangidwa kumaonekera mu mphamvu zisanu. Mwaona? Pomwe pano inu simungakhoze—inu simungakhoze kumugwira Mulungu ndi manja anu monga *chomwecho,* inu simungakhoze kumuona Mulungu ndi maso anu. Iye sanakupatseni iwo kwa inu kuti muzichitira izo. Ndinu . . .

80 Kodi inu munayamba mwamumva woyera mtima wachikulire akumwalira, pamene iwo ankati, "Amayi awo apo, ine sindinawaone iwo kwa zaka." Kodi inu munayamba mwamvapo izo pamene anthu . . . ? Mukuona, chimene icho chiri, maso awa akuziralira kutali ndipo maso auzimu akukhazikika mmenemo. Mwaona? Ndiyeno nthawizina ngati ife . . . ngati Mulungu atazipanga chotero . . . ife timaona masomphenya pomwe maso achilengedwe awo amaziralira kutali. Patsogolo pathu pomwepa, ife tikuyang'ana mwachindunji ndithu, ndipo apo pali masomphenya patsogolo pathu akuonetsa zinthu zauzimu za Mulungu. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

81 Chotero ndiye, penyani, "Pamene msasa uwu wapadziko pano . . . " Tsopano, ena a inu akazi ndi amuna pano mukuyamba kukalamba. Penyani, "Pamene wapadziko uwu . . . " Ine ndikuganiza za ababa okalamba apo, ausinkhu wa zaka nainte thuu. "Pamene msasa wapadziko uwu uli kusungunuka, alipo munthu wauzimu, thupi lauzimu likutidikirira ife limene silingakhoze kuwonongeka." Ine ndidzakakuonani inu kumeneko. Ine ndidzayenda kubwera . . .

82 Ine sindingathe kukamukhudza M'bale Neville umo—umo kumwamba uko, pakuti Yohane anawaona iwo ndipo iwo anali miyoyo pansi pa guwa, ikulira, "Mpaka liti, Ambuye, mpaka liti?" Inu mukudziwa chifukwa chake, ife tinapitamo kudutsa mu Chivumbulutso. Ndi momwe kuti mkati umo iwo ankalakalaka kuti abwerere ndi kukavekedwa ndi matupi achivundi. Iwo anali kulira, "Mpaka liti, Ambuye?"

83 Tsopano, iwo ankadziwana wina ndi mzake, koma iwo sakanakhoza kuyankhula ndi kugwirana chanza, kapena ine ndikulingalira iwo amakhoza kuyankhula, koma iwo samakhoza kugwirana chanza ndi zina zotero. Apa pali chifanizo choti chitsimikizire izo. Pamene mfiti ya ku Endori inaitanitsa mzimu wa Samueli, ndipo Sauli anayang'ana pa iye ndipo iye anamuzindikira iye kuti ndi Samueli. Ndipo Samueli anamuzindikira Sauli ndipo anati, "Chifukwa chiani iwe unandiitana ine kundichotsa ku mpumulo wanga, powona kuti iwe wasandulika mdani wa Mulungu ndipo Mulungu wachoka kwa iwe?" Kodi Izo ndi zolondola? Ndipo apo anaima Samueli wakaleyo atavala mwinjiro wake wauneneri, ndipo iye anayang'ana pa iye. Iye anali mu suti.

84 Mfitiyo inamuona iye ndipo inagwera pansi, niti, "Ine ndikuona milungu ikuuka kuchokera mu dziko."

Iye anati, “Chifukwa chiani iwe unandisokoneza ine?”

Ndipo iye anati, “Chabwino, ine ndikufuna kuti ndidziwe momwe nkhondo ikuyendera.

85 Anati, “Mawa iwe ukafa mu nkhondo,” ndipo ana ake akatero, “ndipo pa nthawi ino mawa usiku iwe udzakhala uli ndi ine.” Mwaona? Tsopano, iye anali moyo, ndipo iye ankaoneka monga momwe iye ankachitira pamene iye anali pano pa dziko, kwa mfiti ija imene inali itaima, ikuyang’ana pa iye, ndi Sauli.

86 Tsopano, zindikirani. Nthawi zambiri. . .Bwanji ababa kapena amayi pamene iwo anali kumwalira ndipo anawaona okondedwa awo ataima pamenepo? Iwo anawazindikira iwo. Koma izo ziri mu thupi lauzimu.

87 Koma tsopano pano pali gawo laulemerero. Pa kubwerera kwa Yesu pa chiukitso, si lidzakhala thupi limenelo. Thupi ilo pamenepo, lomwe liri lauzimu limene Mulungu analilenga pa chiyambi, ilo lidzabwerera ku dziko kuti lidzatenge thupi lina, losabadwa ndi mkazi, koma lolengedwa ndi Mulungu (Aleluya!), kuti lisadzakalambe konse kapena kukhala ndi makwinya, osakhala konse ndi tsitsi laimvi pa mutu panu, koma kukakhala wangwiro, kwanthawizonse! Aleluya! O M’bale, izo zingandipangitse ine kufuula pa usiku wotentha! Uko nkulondola! O, mwinjiro wa mnofu uwu ine ndidzaugwetsa, ndi kuuka ndi kutenga mphoto yosathayo! Nchiani mu dziko chomwe ife tingati kuzidandaula nacho?

88 Apo pali dongosolo lonse liri pomwepo, momwe Mulungu anandilengera ine pa chiyambi. Ine ndinabwera kuno pa dziko lapansi, ndinatenga malo anga ngati mlaliki wa Uthenga, kapena inu ngati mwamuna kapena mkazi ndi chipulumutso, ife tikukhala moyo mwa chisomo cha Mulungu. Aleluya! Ndipo mzimu womwewo umachoka kuno umene unalipo kumbuyoko pa chiyambi. Ine ndidzapita kubwerera uko ndi chikumbumtima cha kudziwa kuti ine ndinali kuno, (Aleluya!) ndiyeno nkumakadikira kumeneko pansi pa guwa odalitsika kwanthawizonse, mu mpumulo ndiyeno pamene tikubwerera, ine ndidzalitenga thupi langa pa chimake pomwe pa ubwino, imfa isanaligunde ilo konse.

89 Imfa imakugundani inu pafupi usinkhu wa zaka makumi awiri ndi ziwiri kapena makumi awiri ndi zitatu, inu mumayamba kulefuka. Inu si mulinso mwamuna yemwe inu munali ndi mkazi yemwe inu munali, inu mukafika cha mu makumi awiri ndi zisanu, chinachake chimalowa umo. Makwinya amayamba kubwera pansi pa maso anu. Inu simungakhoze kusamba monga inu munali kuchitira. Makumi atatu, inu mukhoza kuzizindikira izo mochuluka kwambiri. Yembekezani mpaka inu mufike ku makumi anai, monga ine, ndiyeno inu mumazizindikira izo kwenikweni. Koma, O m’bale! Yembekezani mpaka ine ndifike makumi asanu ndi atatu,

makumi asanu ndi anai, ndi pa ndodo iyo, ndiri pamenepo. Ndi chiani icho? Mulungu anangondiika ine mu liwiro kuti azithamanga. Koma tsiku lina laulemerero. . . Iyo ndi imfa ikulowerera umo.

90 Ine ndinali poyamba wamapewa owongoka, ndinali ndi tsitsi lakuda (ndi mutu wodzala ilo), ndi wopanda makwinya pansi pa maso anga; ndipo tayang'anani pa ine tsopano, kukhwinyata yense, mapewa kumagwa, kuyamba kunenepa, ndi makwinya pansi pa maso anga, mutu wa dazi. Bwanji, tayang'anani chimene imfa ikuchita kwa ine kwa pafupi mu zaka makumi awiri zapitazi. Imfa ikuchita zimenezo. Yembekezani mpaka ine ndifike makumi asanu ndi atatu, ngati Mulungu andilola ine kukhala moyo, ndipo mupenye chimene ine ndizioneka ngati, kuimirira monga chonchi pa ndodo yakale, kumanjenjemera monga choncho penapake. Koma, aleluya, tsiku lina laulemerero, imfa idzatenga muyezo wake wonse. Ndiye pamene ine ndidzauka mu chiukitso, ine ndidzakhala chimene ine ndinali, chomwe Mulungu anandipanga ine pa dziko lapansi pano pa ubwino wanga, zediwo, mu thupi osati lopangidwa ndi Akazi a Branham ndi bambo Branham, koma lolengedwa ndi Mulungu Mwiniwake; lomasuka ku chiyesero, lomasuka ku tchimo, lomasuka ku china chirichonse, osadzakhalanso ndi nthenda, kuwawa mtima. O, mai!

91 Ndiye ine ndidzagwira timanja ta mkazi wanga tating'ono, ndi kumayenda chotsika kupyola mu Paradaiso wa Mulungu monga choncho, mwatsopano. Inu mudzachita chinthu chomwecho. Osati mkazi wokalamba wa mutu wa imvi amene inu mukumutsogolera pozungulira usikuuno, kumamutcha mkazi wanu, koma iye adzangokhala wokongola monga iye analiri tsiku lomwe inu munamukwatira iye pa guwa. Aleluya! Fyuu! Izo ndi zokwanira kumupangitsa munthu kufuula. Si choncho? Mwaona?

92 Chabwino, ndiko kulumikizanako. Mulungu ali wotsimikiza. Mulungu akapanga malingaliro Ake kuti achite chirichonse, icho chiyenera kuti chikhale. Satana anaononga chithunzi ichi, ndi chilakolako cha kugonana, kudzera mwa mkazi, kuti azibala ana. Iye anaononga icho. Kotero pitiririani mtsogolo ndi kukachikonza icho, izo zonse ndi zabwino. Malo okhalamo awa ayenera kutenga izi, chifukwa chinthu chokha chimene inu mumachita mu moyo uwu ndicho kuti mutenge mapangidwe anu ndi chifanizo, chomwe inu muli. Ngati inu muli wofiira mutu pano, inu mudzakhala wofiira mutu apo. Ngati muli wakuda mutu pano, inu mudzakhala wakuda mutu apo. Mukuona, chomwe inu munali pa ubwino wanu. Ndipo ngati inu. . . Satana anasokoneza chithunzi, inu simunapeze konse. . . chimene Mulungu analinga kuti inu mukhale, inu mudzakhala. O, nzaulemerero bwanji! Uyo ndiye munthu wanu.

93 Tsopano Genesis 2. Titi, ine ndiyenera kuti ndifulumire, ine ndidzawatenga iwo. (Inu muli ndi chinachake? Inu muli nacho? Inu munatenga aliwonse? Muli nao oti ayankhidwe?) Chabwino, Genesis 2:18-21:

2. Mulungu anamupanga Eva kuchokera ku nthiti ya Adamu, Genesis 2:18-21. Kodi Mulungu analenga amuna ndi akazi, ndiye nkupanga Adamu ndi Eva—Eva?

3. Ndipo kodi Kaini anapita ku chilengo chokha cha mwamuna ndi mkazi mmalo mwa mkazi wake?

94 Tsopano, tiyeni tsopano . . . Ine sindiri . . . Munthuyu mwina alipo amene analemba izi. Tsopano, pamene Mulungu . . . Mu funso loyambali apa.

Kodi Mulungu anapanga amuna ndi akazi, a Genesis 2:18-21?

95 Iai. Ine—ine . . . monga—monga inu muti muone apa, 2:18-21 tsopano, zindikirani:

> *Ndipo YEHOVA Mulungu anati, Si zabwino kuti . . . mwamuna akhale ali yekha; Ine ndimupangira iye mzake wothandizira kwa iye.*
>
> *Ndipo kuchokera mu nthaka YEHOVA . . . anapanga chirombo chirichonse* . . . ndi zina zotero.

96 Tsopano, Mulungu anapanga Eva kuchokera mmbali ya Adamu. Mkazi ali ndi nthiti imodzi yochulukirapo mu thunthu ndi mapangidwe ake kuposa momwe mwamuna aliri, chifukwa nthiti inatengedwa kuchokera mthupi la Adamu. Adamu anali atapangidwa kale ndipo anali wamoyo, ndipo anali wosungulumwa, ndiyeno Mulungu anati, "Si ziri bwino kuti mwamuna azikhala yekha."

97 Chotero ansembe awa ndi ena otero amene amakanizidwa ufulu wa kukhala naye mkazi. Tsopano, izo, mpingo wa Roma ukhoza kuchita chirichonse . . . Awo ndi iwo, iwo ndi omwe ayenera kuyankhira pa izo—chifukwa cha izo, osati ine.

98 Chabwino, ine ndinafunsidwa ndi m—mwamuna, posachedwapa, anati, "Kodi inu mukuganiza bwanji?" Wansembe, anati, "Kodi inu mukuganiza bwanji za wansembe wamng'ono uyo mu mzinda muno amene anamutenga mkazi uja, msungwana uja, msungwana waku Jeffersonville kuno, ndipo anapita kukamukwatira iye?" Mu mpingo wa chi Airishi, inu mukukumbukira. Ine ndaiwala lomwe linali dzina lake.

99 Ine ndinati, "Iye ali nao ufulu wochuluka wa kuti akwatire monga ine ndiriri nawo. Izo ndi ndendende zomwe ine ndikuganiza za izo." Ine ndinati, "Chinthu chokha ine ndikugwira . . . ine ndikuganiza iye anachita molakwika, iye anayenera kupita ku mpingo, ndi kusiya udindo wake, ndiyeno nkupita ndi kukamkwatira msungwanayo mmalo mongothawa monga choncho."

100 Tsopano, inu mukukumbukira pamene izo zinachitika masabata angapo apitawo muno mu Jeffersonville; wansembe wa chikatolika wachi Airishi kumunsi kuno. Iye ndi mnyamata wamng'ono, ndipo iye anali kupita . . . anali ndi mtsikana wina wokondeka wake kumunsi kuno. Ndipo pamene iye . . . Iwo anampatsa iye chopereka chachikondi chochuluka kwambiri, anali akupita kukasinthana maparishi naye, kumutumiza iye uko ku Indianapolis kwinakwake. Ndipo iye anangotenga chopereka chachikondicho, msungwana ndi zonse, ndipo anachoka ndipo anakakwatirana, ndipo iwo sanamvenso konse kuchokera kwa iye ayi. Chabwino, iye anali nawo ufulu kuti akwatire, koma iye analibe ufulu kuti achite izo. Iye sakadayenera kuchita zimenezo. Iye akadayenera kupita ku—mpingo ndipo akanati, "Pano, ine ndikusiya udindo uwu ngati wansembe. Ine ndikupita kuti ndikakwatire, ndipo izo zakhazikika."

101 Koma, tsopano, Mulungu kumupanga Eva, ndi—ndi Adamu ndi Eva pa nthawi yomweyo, chinthu chokha Iye anachipanga chinali chauzimu, Adamu wamzimu ndi Eva wamzimu, mwamuna ndi mkazi. Ndiye, Pamene Iye anapanga . . . anamuika Adamu mkati umu, sizinali zabwino kuti . . . Mukuona, icho ndi chithunzi cha Mulungu kufutukulidwa nthawi zonse. Chirichonse monga ichi, icho chikungo—icho chikungobwera mpaka pansi, kungomafutukulika kwathunthu kumene, kubwera mpaka ku zakachikwi mpaka uko ndi kumangopitirirabe mpaka mu Umuyaya. Chithunzi cha Mulungu basi chikungofutukulika, Mulungu kudzifutukula Yekha.

102 Pano, Mulungu anadzionetsera Yekha mwa Khristu Yesu, kukaonetsa chomwe Iye anali. Yesu anali chiani? Mwamuna wa zisoni, wodziwa zowawa, wokonda. Kwa wachiwerewere, "Ali kuti okutsutsa ako?"

"Ine ndiribe nnena mmodzi, Ambuye."

"Ngakhale ine sindikutsutsa iwe. Pita usakachimwenso."

103 Wotopa ndi wolema pa kuyenda pafupi mailosi makumi atatu tsiku limenelo, kudutsa mchenga wa mchipululu ndi zinthu; uko kunali mkazi wa ku Naini akubwera uko; ndi mnyamata wake yekhayo, wakufa atagona pamenepo. Iye anaimitsa gulu la malirolo, naika manja ake pa iye, anati, "Uka." Ndipo mnyamata yemwe anali wakufa anauka aponso. Uyo—Uyo ndi Ambuye wathu Yesu. (Zikomo inu, Teddy, mwananga) Ndipo apo, uyo anali Ambuye wathu Yesu. Iye sanali wotopa kwambiri, sanali wolema kwambiri kuti achite chirichonse chabwino. Chabwino.

Tsopano pano pali chinthu china:

Kodi kaini anapita ku—ku cholengedwa choyamba cha mwamuna ndi mkazi ngati mkazi wake?

104 Tsopano, apo pali funso lovuta zedi, tsopano mvetsetsani mwatcheru kwenikweni. Tsopano, o, ndiri. . .inu mwaonapo anthu atazilemba mu pepala, "Kodi Kaini anakamtenga kuti mkazi wake?" O, ine ndinkakonda kuzinena izo.

105 Ndipo ine sindinali kuphunzitsa za gehena yoyaka kwa pafupi zaka zinai pambuyo pa kutembenuka kwanga. Ine ndinkayenera kuti ndiziwone izo mu Lemba. Ngati ine sindikuchidziwa, ine sindinena kanthu za icho. Mwaona?

106 Koma, tsopano, "Kodi Kaini anamutenga kuti mkazi wake?" Tsopano, ndiko—kusanthula kwa funso ili tsopano. "Ndipo kodi Kaini anapita kwa mkazi wake ku chilengedwe cha mwamuna ndi mkazi, ngati mkazi wake?" Mwaona? Tsopano, tsopano, mmodzi wa oyamba. . .

107 Akazi a DeArk awa, inu nonse mudamva za machiritso awo usiku wina momwe Mulungu anawadalitsira iwo ndi chirichonse. Iwo anali atagona, akufa, iwo anabwera cha uko mma 2 koloko mmawa.

108 Ndipo chotero, tsopano, ndi momwe ine ndinadzera. . . Mnyamata wawo George, mnyamatayo anali wamizimu, Ed, nayenso. Iwo anali mu sitolo, ndipo ine ndinamva zokambirana kumbuyo uko, kumene woyamba. . . kumene Kaini anakatenga mkazi wake. Chabwino, mmodzi yemwe anali kupambana ankawoneka kuti anali nako kutsutsa kwabwino, iye anati, "Ine ndikuuzani inu kumene Kaini anakatenga mkazi wake," anati, "Kaini anapita uko ndipo anakakwatira chinyani chachikazi chachikulu kwambiri." Ndipo anati, "Kuchokera kwa chinyani icho kunabwerako mtundu wachikuda." Anati, "Inu mukuzindikira mutu wa munthu wachikuda ndi wokhala ngati wosongoka monga *choncho,* monga—monga nkhwere aliri, mmutumo."

109 Chabwino, ine ndinaima apo, ine ndinali pafupi miyezi iwiri yokha mu Uthenga. Ine ndinati, "Ine sindikufuna kusiyana ndi inu bambo, chifukwa ine sindine wophunzira, ine ndangopulumutsidwa kumene. Koma" Ine ndinati, "ngati izo ziri chomwecho, ndiye mtundu wachikuda wa anthu ukadaleka kukhalapo pamene chiwonongeko cha chigumula, pamene dziko linawononggedwa ndi madzi, pakuti Nowa ndi banja lake anali okhawo omwe anali mu chombo. Iwo anali okhawo omwe anali mu chombo. Mtundu wachikuda ukadaleka kukhalapo," ine ndinati, "ngati izo zikadakhala ziri choncho." Ine ndinati, "Ayi, bwana! Mtundu wachikuda sunadze kuchokera kumeneko. Ayi, bwana. Mtundu wachikuda uli wochokera ku mtengo womwewo womwe ife tachokerako, ndi munthu aliyense yemwe alipo, umodzi womwewo." Palibe kusiyana. Ndendende. Ife tangokhala tonse. . .Wina akhoza kukhala wachikasu, ndi winayo wa bulauni, wina wakuda, ndi winayo woyera, ndi wina wotuwa ndi wina wofiira ndi basi monga choncho, koma ndinu nonse

ochokera ku mtengo womwewo. Ndilo gawo chabe lathupi kunja kuno. Ndiko kulondola. Ndinu munthu mofanana basi, olengedwa kuno ndi Mulungu.

110 Ndipo tsopano, zindikirani, kuno osati kale litali, nditaima cha uko ndi madokotala ena mu Louisville, ine ndinali kuyankhula za mu Afrika momwe anthu osauka awo, mtundu wodya amzao, makamaka, momwe iwo anali ndi mkazi uko, anatenga kakhanda kakang'ono, anapeza kakhanda kakang'ono, ndipo—ndipo anali atakamenya iko monga choncho ndipo anakamangirira iko kuthengo ndi kukasiya iko kaole kwa masiku angapo, inu mukudziwa, mpaka iko katakhala katavunda iwo asanakadye iko, inu mukudziwa. Chirichonse monga choncho, iwo amakasiya iko kavunde kanthawi pang'ono, kamafewa.

111 Musati muganize kuti izo ndi zochuluka kwambiri za odya anzawo. Mu England iwo amachita chinthu chomwecho, iwo amapha nkhukutembo ndi kuipachika iyo mu mitengo, chotero kuti nthenga zikangoti zagwa kwa iyo ndiye iwo amaidya iyo. Ndiwo manthu wa mtundu wa anthu achingelezi achi saxon, mu England. Nkulondola uko. Ndipo musati muganize . . . Inu simusowa kuti mupite ku England, mungopita kumusi kuno mu maiko akummwera, inu mukapeza chinthu chomwecho. Ndithudi. Munthu aliyense angakhoze kudya nkhono kapena—kapena njoka yambobo, akhoza kudya china chirichonse. Chotero . . . Eya.

112 Tsopano zindikirani, ndiroleni—ndiroleni ine ndikuuzeni inu. Koma, ichi ndi chimene chinachitika. Achikuda . . . m—mtundu wachikuda ulibe kanthu kochita ndi ichi. Kaini . . .

113 Tsopano, ine ndikufuna inu kuti mupenye. Iwo ananena kuti, "Iye anapita ku dziko la Nodi." Tsopano, Kaini anali mu Edeni. Ndipo Edeni, Munda wa Edeni, unali kummawa kwa Edeni. Nkulondola uko? Munda wa Edeni unali kummawa mu Edeni, mmbali ya kummawa kwa Edeni. Ndipo Akerubi anaikidwa, ndipo Mtengo wa Moyo unali ku chipata cha kummawa kwa Mundawo, ndipo uko ndi kumene ine ndikuganiza Kaini ndi Abele anakapanga nsembe zao. Ndipo kumeneko ndi kumene Mkerubi wa lupanga lamoto sakanakhoza kuwalola iwo kulowa umo aponso, kummawa kwa chipata!

114 Kodi inu munazindikira, Yesu adzabwera kuchokera kummawa. Kuwala kumatuluka kuchokera kummawa. Chirichonse chimabwera . . . Chitukuko chinayambira kummawa ndipo chikupita kumadzulo, mpaka icho chikuzungulira zungulira ndi kudzadzipeza chokha kachiwiri. Ife ndife Chigawo cha Kumadzulo. Icho ndi Chakummawa, Chakummawa ndi chitukuko chakale kwambiri. China ndiye chitukuko chakale kwambiri chimene chimadziwika, ndi azambiriyakale, mu dziko lero. Kummawa!

115 O, momwe ife tikanakhoza kukhalitsa pa mafunso awa kwa maora, pa limodzi, koma izo sizikanati basi enawo. Koma zindikirani, pano pali . . . Ndi angati akanafuna kuti adziwe chimene ife timakhulupirira za Kaini, kumene ndi yemwe anali mkazi wa Kaini? Tiyeni tione. Chabwino. Ine ndikuuzani chimene Kaini anachita, ndipo ndi yankho lokha lomveka inu mungakhoze kulilingalira: Kaini anakwatira mlongo wake yemwe. Iye adayenera kutero, pakuti uko kunali wamkazi mmodzi yekha pa dziko lapansi apo; Baibulo limangopereka umboni wa atatu kukhala atabadwa, Hamu, Shemu . . . kapena osati . . . Ine ndikupempha chikhulukiro chanu, anali Kaini, Abele, ndi Seti. Koma ngati uko kunalibe aliyense . . . Baibulo sikwenikweni kuti amalemba kubadwa kwa msungwana. Inu mukudziwa izo.

116 Tsopano, ine ndikutsimikiza ndikuwatola akazi usikuuno. Koma, penyani, dziko limapembedza akazi, koma akazi anali chida cha Mdierekezi pa chiyambi. Ndipo wosalungama lero ndi chida chopambana chomwe ali nacho. Iye adzatumiza alaliki ochuluka ku gehena kuposa malo onse ogulitsa mowa amene alipo mu dziko. Mulole kahule kakang'ono kali ndi ndudu pa ngodya ya kamwa yake, ndi tsitsi lake atalinyolola lonse monga choncho, ndipo nsidze zazitali zazikulu zimene zimaphethira mmwamba-ndi-pansi, m'bale, kakang'ono . . . kathupi kooneka ngati kabwino mmapangidwe pa iye, penyani chimene iye ati azichita.

117 Mlaliki, iwe kulibwino udziphimbe wekha ndi Mwazi wa Yesu Khristu. Ndi kulondola. Tsopano, inu musati mundiuze ine, ndinu mwamuna! Ine ndaona zochuluka kwambiri za izo. Tsopano, penyani pano. Chinthu chabwino kuchichita ndi kuyika malingaliro ako mokhazikika pa Yesu Khristu ndi kulola maganizo ako akhale angwiro.

118 Monga Paulo ananena uko mmenemo, anati, "Ndicho . . . Ife tikudziwa kuti ife tiri nayo mphamvu kuti timutsogolere mlongo. Ine ndiri nayo mphamvu kuti ndichite izo, koma" anati "Ine sindikanati ndichite izo." Mukuona, iye sakanati achite izo. Iye anati, "Ine ndikudziwa kuti utumiki uyenera kumakhala moyo ndi zao—zao . . . Osati kuipanikiza ng'ombe imene ikupuntha chimanga."

119 Inu mukudziwa, ife nthawizina timaganiza, popeza ndife mlaliki . . . (Osati inu ndi ine, ine sindikunena, m'bale) Koma alaliki amaganiza chifukwa iwo ndi alaliki kuti—kuti iwo ali winawake wamkulu kuposa mmodzi wa mamembala wamba a mpingo. Inu si wamkulu ayi ndipo inu simuli konse woposa pamaso pa Mulungu kuposa chidakhwa chija chimene chinatembenuzidwa ora lapitalo.

120 Ndicho chinthu chimodzi chimene kukonzanso sikunachotse konse, chinali zinthu izi. Ine ndikudziwa ine ndimasaina

dzina langa "Reverendi." Ndizo ndendende, icho ndi chabe c—chinthu chachizolowezi cha lero, koma izo sizimayenera kuti zizichitidwa. "Reverendi" ndi "Bishopu" ndi "Dokotala" ndi zinthu zonse izi ali maudindo opangidwa ndi anthu, ndipo izo ndi zamkhutu! Mu Baibulo iwo anali "Petro," "Yakobo," "Paulo," "Yohane," ndi ena onse a iwo.

121 Paulo anati, "Tsopano, pano, ine ndikudziwa ine ndimalalikira Uthenga, iyo—iyo—iyo ndi ntchito yanga." Ine ndine mlaliki, iye ndi mlaliki, M'bale Neville ndi mlaliki, koma iyo . . . Ndiyo ntchito yathu, ndikuti tikhale mlaliki. Chabwino, ndicho basi chimene ife tikuyenera kumachita. "Koma mundirole ine ndichite chinachake," Paulo anati, "izo nzopitirira apo." "Tsopano, ine ndiri nawo ufulu kuti ndizitenga ndalama," Paulo anatero, "Koma ine ndizipanga mahema basi kuti ndikuonetseni inu ine ndikhoza—ine ndikhoza kudzipereka." Iye anati, "Ndi zolemekezeka, ukwati ndi wolemekezeka pakati pa onse, makama osadetsedwa. Ndi zabwino kuti mwamuna azikwatira." Iye anati, "Ine ndiri nawo ufulu woti ndikwatire. Tsopano, ine—ine ndikhoza kukwatira, ine ndiri nawo ufulu mwalamulo kuti ndikwatire. Koma ine sindikwatira basi, ine ndikufuna ndichitepo kudzipereka kwina kwa Ambuye." Mwaona? Ndiye Iye anati, "Munthu aliyense amadziwa maitanidwe ake. Msiyeni iye azichita monga . . . Ena ndi ofulidwa chifukwa cha Mawu a Mulungu, ndi zina zotero."

122 Ife timafuna kuti tichite chinachake kupyola ntchito yathu. Ndipo ngati inu muli obadwa kachiwiri kwenikweni ndi Mzimu wa Mulungu ndi kuti, "Chabwino, ndi ntchito yanga kupita ku tchalitchi, ine ndikulingalira ine ndiyenera kuti ndipite." O, mayi! Chabwino, ine ndikufuna kuti ndichite zoposa izo, ine ndikufuna kuti ndipindulire miyoyo ina kwa Khristu. Ine ndikufuna kuti ndichite chinachake! Ine ndikufuna ndizikawachezera odwala kapena kumuchitira Iye chinachake. Ndi ntchito yanga kulalikira maliro, ndi ntchito yanga kulalikira Uthenga, ndi ntchito yanga kuwapempherera odwala. Ndisiyeni ine ndichite chinachakenso, mundirole ine ndipite kunja ndi kukachita chinachake chomwe Mulungu ati andilemekeze ine nacho.

123 Tsopano, tibwerere kwa Kaini. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Pakuti Eva anali chachikazi chokha chimene chinalengedwa ndi Mulungu, ndipo ngati iye analibe ana aakazi aliwonse, pamene mkazi wotsiriza uyo (wamkazi yekha) anafa, mtundu wa anthu ukanaleka kukhalapo. Ndi kulondola uko? Kukanakhala kulibe akazi enanso. Chotero iye ayenera kuti anali nawo ana aakazi. Ndipo Kaini anakwatira mlongo wake yemwe, chifukwa iye ankayenera kuti atero, kunalibe malo ena oti akazi adze kuchokerako.

124 Ndipo icho chinali chovomerezeka ndi chololezedwa mu masiku amenewo, ngakhale mpaka kwa Abrahamu, ndipo

ngakhale mmusi mpaka kwa Isaki. Isaki anakwatira msuweni wake yemwe wa magazi. Ndipo Abrahamu anakwatira mlongo wake yemwe, mlongo wa magazi. Wa abambo ake. . . Ndi amayi osiyana koma bambo yemweyo. Ndipo nyongolosi imabwera kuchokera ku chiwalo chachimuna. Sarah, amene anabala Isaki wodabwitsayo. Ndi kulondola uko? Panali popanda aliyense pa dziko lapansi apo.

125 Izo zonse zinali mwa choimira, kuonetsa kuti. . . Ndi ichi pano, m'bale! Isaki. . . Rabeka ndi woimira Mpingo, ndipo Isaki ndi woimira Mkwatibwi, Khristu. Ndi kulondola uko? Ndipo iwo ayenera kukhala achibale cha Magazi! Aleluya! Ameni! Achibale cha Magazi!

126 Chotero Kaini anakwatira mlongo wake, ndipo izo. . . Ndiye iwo anapita cha uko mu dziko la Nodi. Tsopano, ife tikufika mu phunziro lozama ngati ife titi tipite patsogolo pang'ono, ndipo ine ndiri wokondwa kuti inu simunafunse mopitirira mulimonse kuposa apo, (monga, "Ziri kuti zimphona zija zimene zinali mdziko lija tsiku ilo?" Josephus ndi ena osiyana ali ndi zotsutsa zambiri pa izo). Ameni! Ngati ine sindinalitenge ilo molondola, m'bale, mudzaliperekenso ilo muno kachiwiri Lamlungu mmawa. Chabwino.

4. Kodi inu mungafotokoze Lamlungu liri tsiku loyamba la sabata ndi Loweruka liri tsiku lachisanu ndi chiwiri? Akhristu amapita ku tchalitchi Lamlungu, tsiku loyamba la sabata. Kodi iwo samayenera kumapita Loweruka, tsiku la chisanu ndi chiwiri la sabata?

127 Chabwino, tsopano, bwenzi lokondeka, yense yemwe anafunsa izo, ilo ndi funso labwino kwambiri. Ilo ndi funso lakale limene limatsutsidwa pakati pa zikwi za ophunzira lero, koma ndingathe, mungondilola ine ndipereke momwe ndidziwira, inu muone, ndi zonse zomwe ine ndingakhoze kuchita. Ndipo ngati ine sindiri kulondola, chabwino, inu—inu mupilire nane, ndipo Mulungu andikhululukire ine, inu mukuona, ngati—ngati ine nditi ndizipange izo molakwika.

128 Tsopano, malingana ndi lamulo. . . Tsopano, muli mwina munthu wa Seventh-day Adventist atakhala muno. Uko kunali kuphunzira kwanga koyamba, kunali Seventh-day Adventist. Ndiko kulondola. Kunali ku Seventh-day Adventist, kumene ine ndinaphunzira moyambirira. Ndipo pamene iwo anabwera ndi nadzandiuza ine kuti "Loweruka linali tsiku lachisanu ndi chiwiri," m'bale, izo zinali molingana ndi kalendala ya Chiyuda. Ndipo Kalendala ya Chiroma siinazikonze izo apo, ndipo Loweruka kwenikweni linali loti likhale Lamlungu. Chabwino, iwo anali atandigulitsa ine pa chinachake chomwe ine ndinkaganiza chinali cholondola. Ndipo utali wonse pamene ine ndinali kuwerenga zolemba zawo ine ndinati wovomereza kumene izo, zana pa zana, koma tsiku lina ine ndinalitenga

Baibulo ndipo ine ndinaona kuti izo zinali zosiyana ndiye. Mwaona?

129 Tsopano, Loweruka ndi tsiku la sabata monga mwa kuzungulira kwa sabata. Tsopano, ife sitikudziwa. Izo zasinthidwa, ndipo ife tiri nako kusintha kochuluka kwambiri iwe sungadziwe konse basi lomwe ilo linali. Mwaona? Chifukwa ife . . . Tsopano, Ayuda amadzinenera kuti ife tiri basi pafupi . . . tiri pakali pano cha ku 1970 chinachake, molingana ndi kuzungulira kwawo, kalendala yao. Kalendala ya Chiroma ikuzitenga ngati 1953. Ndipo iwo anali ndi kalendala inanso imene imachitengera icho kwinakwakenso. Koma icho ndi chomwe chimapangitsa icho chitsimikiziro cha Chikhristu, izo zonse maziko ake ali pa kubadwa kwa Khristu. Inu mukuona, ndi kumene ife timazitengera izo.

130 Tsopano, koma tsopano monga tsiku lachisanu ndi chiwiri, tsopano, alipo anthu ambiri Achipentekoste amene ali sabata—sabata asabata, amasunga sabata la Loweruka. Tsopano, iwo amati, "Mulibe Mawu mu Baibulo oti inu muzisunga Lower- . . . Lamlungu ngati tsiku." Tsopano, ine ndinena chinthu chomwecho pa sabata mu Chipangano Chatsopano. Mwaona? Tsopano, Loweruka linali tsiku la sabata limene linapatsidwa kwa Ayuda. Tsopano, ilo linangoperekedwa mu kadanga.

131 Tsopano, ichi chikhoza kuutsa funso lina kuti likawombedwe mobwezera pa ilo. Koma, tsopano zindikirani. Pamene Mulungu anapuma pa tsiku lachisanu ndi chiwiri, ndiye tsiku lachisanu ndi chiwiri silinali kusungidwa, monga—malingana monga momwe ine ndikudziwira mu Lemba, kupitirira mpaka pafupi zaka fifitini handiredi. Ndipo mu chipululu, Mulungu anamupatsa Israeli tsiku lachisanu ndi chiwiri ngati chizindikiro pakati . . . Mulungu.

132 Ndipo Mulungu anapuma tsiku lachisanu ndi chiwiri, chikumbutso Chake cha tsiku la mpumulo. Ine ndikunena izo monga choncho mwa phindu lakuti uyu akhoza kukhala m—m'bale kapena mlongo wa Seventh-day Adventist, mukuona, ndipo iwo ali ndi mpingo wokondeka. Ndipo tsopano zindikirani, ine ndikhoza kusiyana ndi iwo pang'ono pokha pa—pa funso ili.

133 Tsopano, Mulungu analiyeretsa tsiku lachisanu ndi chiwiri. Masiku asanu ndi limodzi anali a munthu. Tsiku lachisanu ndi chiwiri linali tsiku la mpumulo wa Mulungu, limene linali choimira, choimira cha Zakachikwi. Tsopano, tsopano, zindikirani ichi, momwe—momwe zikugwirizanirana umu. Tsopano pamene Yesu anabwera ku dziko lapansi, chimene chinampachikitsa Yesu chinali kuti Iye sanali kusunga tsiku lasabata; mirandu iwiri yokha imene iwo anali nayo momutsutsa Yesu inali kuti "Iye ankaswa tsiku la sabata, ndipo ankadzipanga Iyeyekha Mulungu." Ndipo Iye ankati

Iye anali Mbuye wa sabata. Iye anali . . . Iye analinso Sabata la Mulungu, ndipo Iye anali Mulungu. Kotero iwo analibe njira yomutsutsira Iye.

134 Tsopano, ndiroleni ine ndingokukhazikitsirani inu ichi ndi kukuonetsani inu tsiku limene ife tikuyenera kumalisunga. Tsopano, kodi liripo Lemba? Ine ndifunsa izi kwa phindu lanu:

Kodi liripo Lemba, M'bale Branham, lotiuza ife ndi kutiloleza ife kuti tizisunga Lamlungu monga ngati Ayuda ankasunga Loweruka?

135 Ayi, bwana, palibe ayi. Palibe Lemba mu Baibulo, pakuti mu Chipangano Chatsopano, loti ife tizisunga mwina Loweruka kapena Lamlungu. Koma chifukwa chimene ife timasungira Lamlungu, ndi chikumbutso cha chiukitsiro. Palibe . . .

136 Tsopano, inu munena kuti, "Roma Katolika anachita izo." Iwo amadzinenera kuti iwo anachita izo, koma ngati iwo anachita, Paulo Woyera anali wa Chiroma Katolika, ndipo chomwechonso anali Petro, Yohane, ndi Yakobo, ndi ena onse a iwo, chifukwa iwo ankakomana pa tsiku loyamba la sabata pa kupembedza kwao. Ndipo, molingana ndi azambiriyakale, njira yokha yomwe iwo ankadziwira pakati pa Mkhristu wa Chiyuda ndi Myuda wa chiorthodox (iwo onse ankapita ku masunagoge), koma mmodzi ankapita Loweruka (amene ankakana chiukitsiro cha Yesu), ndipo winayo ankapita Lamlungu (amene ankakhulupirira kuti Yesu anauka kwa akufa). Ndipo icho chinali chizindikiro. Ndipo icho chidzakhala chiri, chikanali chilemba panobe, ndipo icho chikhoza kudzatulukira ndi kukhala chilemba cha chirombo.

137 Tsopano, ine ndikudziwa kuti . . . okondedwa athu abale a Seventh-day Adventist akuganiza kuti icho ndi Chisindikizo cha Mulungu. Iwo ankati, "Inu mumasindikizidwa pa kusunga sabata." Mulibe Lemba mu Baibulo limanena izo.

138 Ndipo apa pali Lemba mu Baibulo limene limanena kuti—kuti iwe umasindikizidwa, Aefeso 4:30, amati, "Musaukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu umene inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu," ubatizo wa Mzimu Woyera.

139 Tsopano ine nditsimikizira kwa inu kuti Chisindikizo cha Mulungu ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Mwaona? Ndiwo ubatizo wa Mzimu, uli Chisindikizo cha Mulungu. Tsopano, Yesaya 28, iye anati, "Langizo liyenera likhale pa langizo, mzere pa mzere, kuno pang'ono ndi uko pang'ono."

140 Tsopano penyani, tsopano, bwenzi wokondedwa. Tsopano, anthu amene amasiya kugwira ntchito . . . Onani, munthu akuyesera kuti apeze chinachake kuti adzipulumutse yekha. Palibe kanthu kamene inu mungakhoze kuchita pa icho. Inu mumapulumutsidwa mwa chisomo. Mulungu amachita kuitanako, Mulungu amachita kupulumutsako. Iwe umangotsatira m—mapazi a Mulungu, ndizo zonse.

Inu simungakhoze kunena. Ndicho chomwe chikhalidwe cha munthu chiri. Iwo amayesa kusiya kudya nyama, iwo amayesa kusunga masiku a sabata, iwo amayesa ku. . . "Ngati inu mungasiye kuchita *izi*." Ndicho. . .Iwe sumapulutsidwa pa kusadya nyama. Iwe sumapulumutsidwa ndi *ichi, icho* kapena *chinacho*. Iwe umapulumutsidwa mwa chisomo! Ndipo Mulungu, mwa chisomo, amakupatsani inu watsopano, Moyo Wamuyaya. Mukuona chomwe ine ndikutanthauza? Ndipo Moyo Wamuyaya ndiwo ubatizo wa Mzimu Woyera.

141 Tsopano ndiroleni ine ndikusonyezeni inu. Kodi mawu oti *sabata* amatanthauza chiani? Aliyense akudziwa, mungokweza dzanja lanu? Sabata? [Mlongo ati, "Mpumulo."—Mkonzi.] Mpumulo. Ndendende. *S-a-b-a-t-a*, tsiku la sabata, limatanthauza "m-p-u-m-u-l-o," tsiku lopumula. Pezani kuwerenga kwanu kwa m'mbali mu Baibulo ndipo muyang'ane, tsiku "Lopumula." Tsopano tiyeni tipite ku Ahebri, mutu wa 4, mwamsanga ndithu tsopano. Ndipo ife tidza . . .

142 Ili—ili ndi funso langa lotsiriza pomwe pano. Ndipo, m'bale, ndiwone ngati M'bale Neville ali nawo iwo apo. Ine ndikudziwa kuti angapo a iwo ndi afupiafupi, kotero ife sitikusungani inu motalika kwambiri. Tsopano, ndikhululukireni ine pamene ine ndikupapeza ipo.

143 Tsopano, pamene inu mukuwaona mawu apa, *mpumulo*, ndiye inu muzidziwa iwo akunthauza "sabata."

144 Tsopano, pano pali Chipangano Chatsopano. Yesu, mu Mateyu Woyera, Iye anayambira pa mutu 5 wa Mateyu Woyera, ndipo Iye akuyamba monga chonchi: "Inu mwanawamvapo iwo akunena, iwo a nthawi zakale, 'Inu musati muzichita chigololo.'" Icho, chinali chiani icho? Lamulo, malamulo. "Koma Ine nditi kwa inu, kuti, aliyense amene ayang'ana pa mkazi ndi kumukhumbira iye." Analisintha ilo, sichoncho Iye? "Inu mudawamvapo iwo akuti, iwo a nthawi zakale, 'Inu musati muzipha,' koma Ine nditi kwa inu!" "Analisintha ilo, sichoncho Iye? (Mumaganiza kuti Iye sanalisinthe lamulo?) Chabwino. Iye anati, "Koma Ine nditi kwa inu kuti aliyense yemwe amukwiyira m'bale wake popanda chifukwa wapha kale." Izo sizinalipo konse mmbuyo pansi pa Chipangano Chakale, icho ndi Chipangano Chatsopano. Iye anangosesa limodzi mpaka kutali kupitirira izo. Mwaona? Iye anapita mtsogolo ndi kukawapereka malamulo awo uko, koma Iye anaphonya, Iye analilumpha lachinai, limene liri tsiku lachisanu ndi chiwiri. Tsopano mu mutu wa 7, pamene Iye . . .

145 Mu Chiphunzitso chapaphiri, pano pali zomwe Iye ananena, Iye anati, "Inu munawamva iwo akunena, iwo anthawi zakale, 'Inu mudza, ndipo inu musadzati,' ndipo Ine nditi kwa inu mosiyana. Inu munawamva iwo akuti, 'Dzino kwa dzino, ndi diso

kwa diso,' koma ine nditi kwa inu! Inu munawamva iwo akunena mosiyana, koma Ine nditi ndi inu!"

146 Tsopano, pa mapeto a izo zonse, Iye anasiya kunja lamulo la 4. Tsopano, ilo linali, "Muzikumbukira tsiku la sabata ndi kulisunga ilo mopatulika." Tsopano Iye anati:

> *Bwerani kwa ine, nonse inu amene mukuvutika ndipo muli olemedwa ndi katundu, ndipo Ine ndidzakupatsani inu mpumulo* kwa solo yanu.

147 Tsopano penyani, "Yense amene achita chigololo ayenera kuti agendedwe," iwo ankayenera kuti achite kukhala ali mkati mwa mchitidwe wa kuchita chigololo. Ndi kulondola uko? Ndipo icho chinkayenera kukhala chikuchitidwa mwathupi. "Yense amene apha," iye ankayenera kukhala wakupha.

148 Koma Yesu anati, "Yense amene ayang'ana pa mkazi," solo yake, mzimu, popanda kanthu ka mu thupi lake tsopano. Solo yake ndi yowomboledwa, iyo sinali apo; ilo linali mphunzitsi, mwaona, lamulo linali. Tsopano Iye anati, "Yense amene ayang'ana pa mkazi namukhumbira iye wachita naye chigololo kale mu mtima mwake." Tsopano Iye anati," Inu munawamva iwo akuti, 'Inu musati muzipha,' koma Ine ndikuti aliyense yemwe amukwiyira m'bale wake popanda chifukwa wapha kale."

149 Tsopano Iye anati, mwa kuyankhula kwina, za sabata, Iye anati:

> *Bwerani* kwa *ine, nonse inu amene mukuvutika ndi olemedwa ndi katundu, ndipo Ine ndidzakupatsani inu mpumulo* kwa solo yanu, sabata kwa solo yanu. (osati kwa thupi logwirika, kwa *solo* yanu)

150 Tsopano, mvetserani—mvetserani kwa Paulo tsopano. Ngati inu mungakhoze basi. . . Ine ndikudziwa, kwatentha ndi chirichonse, kukutentha pamwamba pano, naponso. Koma, tsopano, tiyeni ife timvetse izi mwatcheru tsopano kuti ife tikhale otsimikiza kuti tizikhazikitse izo. Tsopano, Paulo akulembera kwa Ahebri. Ahebri anali ndani? Yankhulani mokweza. Ayuda. Ndi kulondola uko? Tsopano, iwo anali osunga-lamulo, osunga-sabata. Ndi kulondola uko? Ndi kulondola uko, m'bale, mlaliki? Iwo anali osunga-sabata, iwo anali osunga-lamulo. Chabwino.

151 Tsopano, Paulo akuwabweretsa Ayuda, mwa mithunzi ndi choimirira, kuonetsa chimene lamulo linkaimira, 'Lamulo pokhala nawo mthunzi wa zinthu zabwino zakudza," ndipo iye akupita patsogolo ndi kuzipereka izo apo mu malo amodzi ngati mwezi ndi dzuwa. Monga—m—mwezi uli mthunzi chabe wa dzuwa kuwalira pa dziko lina lake kapena mdziko mwinamwake, ndipo ilo likunyezimitsira mmbuyo kuno. Tsopano, koma tsopano, ndipo ilo silikadakhoza,. . . Ahebri 9.

152 Tsopano, zindikirani tsopano mu Ahebri 4, iye akudza ndi chokambapo pa Sabata. Tsopano penyani:

> *Tiyeni ife chotero tiwope, mwina, lonjezo lingasiidwe kwa ife* loti tilowe *mu mpumulo wake,* . . .

153 Tsopano, Paulo akuyankhula kwa anthu a sabata tsopano, anthu amene ankasunga tsiku la sabata. "Tiyeni ife tiwope mwina lonjezo lingasiidwe kwa ife la tsiku la Sabata," mwa kuyankhula kwina. Kapena ngati inu muti muzindikire zowerenga za mmphepete zanu, kapena "kusunga kwa sabata." Ndi "j" mwangamu, za mu Baibulo la Scofield, kapena "kusunga kwa sabata." Mwaona? Chabwino.

> *Tiyeni ife . . . tiwope, mwina, lonjezano lingasiidwe kwa ife . . . kukhala operewedwa ilo.*
>
> *Pakuti kwa ife uthenga unalalikidwa, monganso kwa iwo* (mmbuyo pansi pa lamulo): *koma mawu olalikidwawo sanawapindulire iwo, posakhala atasakanizidwa ndi chikhulupiriro kwa iwo amene anawamva iwo.*

154 Tsopano, ndimo mmbuyo pansi pa lamulo. Iwo analibe chikhulupiriro, chifukwa panalibe chirichonse choti nkukhazikitsapo icho. Mwaona? Chabwino:

> *Pakuti ife amene takhulupirira* kuti *tilowe mu mpumulo* Wake, *monga iye ananena,* . . .

155 Tsopano, mpumulo, "Wake". Tsopano, "Wake," Uwo ndi Mpumulo wa Khristu. Chabwino, Mpumulo Wake, "sabata" Yake. Ndipo nthawi iliyonse ine nditi ndigwiritse ntchito *mpumulo*, walembedwa apa, ine ndizigwiritsa ntchito "sabata" chotero inu mumvetse za kusunga kwa tsiku. Mwaona?

> *Pakuti ife amene takhulupirira kuti tilowe mu sabata* Yake, *mpumulo, monga iye anati, . . . Ine ndalumbira mu mkwiyo wanga,* (kwa Aheberi) *iwo sadzalowa mu mpumulo wanga: ngakhale . . .* (Tsopano, penyani Paulo akupita kukalipanga ilo tsiku loyeretsedwa la Mulungu) . . . *ngakhale ntchito zinatsirizidwa kuchokera pa maziko a dziko.*
>
> *Pakuti iye anayankhula mu malo ena za tsiku lachisanu ndi chiwiri* la mpumulo, kapena sabata . . . (Ndi kulondola uko? Ine ndiziika izo apo, mukuona)
>
> *Pakuti iye anayankhula mu malo ena* (mu chilamulo) *za tsiku lachisanu ndi chiwiri mwa chonchi, Ndipo Mulungu anapumula pa tsiku lachisanu ndi chiwiri ku ntchito zake zonse.*

156 Ndi limenelo tsiku lanu lachisanu ndi chiwiri. Tsopano, Paulo akanati avomereze kuti Mulungu analipereka ilo kwa iwo, ilo linali tsiku lachisanu ndi chiwiri. Ndipo Mulungu anapuma tsiku lachisanu ndi chiwiri, Iye analidalitsa tsiku la sabata, Iye

analipatula ilo, Iye analiyeretsa ilo, ndipo analipanga ilo tsiku la mpumulo. Mulungu anachita izo, ku ntchizo Zake zonse.

> *Ndipo mu malo awa kachiwiri, Ngati iwo ati adzalowe mu mpumulo wanga.* (Yesu akuyankhula)

157 Tsopano, pali sabata lina penapake. Ilo liri pati? Tsopano, kumbukirani ichi apa, "Mpumulo wa Mulungu," tsiku la Chisanu ndi chiwiri lija. Paulo anati, "Iwo anali nalo ilo mu malo enaake." Koma tsopano kachiwiri iye anati, "Ngati iwo ati adzalowe mu Mpumulo Wanga," akuyankhula za Yesu mu Mateyu chabwino.

> *Powona* kuti *uli* kutsalira *kuti ena ayenera kulowa* umo, *ndipo* kwa iwo *amene ilo linalalikidwa koyamba sanalowemo ayi . . . chifukwa cha kusakhulupirira:*
>
> *Kachiwiri, . . .*

158 Tsopano mvetserani mwatcheru! Aliyense akumvetsera, nenani, "Ameni!" [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Mvetserani:

> *Kachiwiri, iye akuika tsiku linalake, . . .*

159 Iye anaika tsiku lina apa. Ilo linali chiani? Aliyense anene ilo nthawi imodzi. Sabata! Ndi kulondola uko? Iye anaika tsiku lachisanu ndi chiwiri la mlungu ngati sabata mu malo awa.

> Ndipo kachiwiri, *iye* anaika *tsiku linalake*, nati mu Davide (mu Masalmo), *Lero, patapita nthawi yaitali chotero;* (mpaka Yesu atadza, inu mukuona, nthawi yoyamba) . . . *izo zinanenedwa, Lero ngati inu . . . mumva liwu lake, musati muumitse* mtima *wanu.* (pali mpumulo wina ukubwera; osati wathupi, *wauzimu*)

160 Tsopano, penyani. O, inu mukuti, "Pamene ife tiri ndi tsiku lachisanu ndi chiwiri, aponso." Tsopano, chigwireni icho miniti yokha. Tiyeni ife tiwerenge ndime yotsatirayi, mwaona, musati muzitenge izo mofulumira kwambiri. Chabwino:

> *Pakuti ngati Yesu akanati awapatse iwo . . . Pakuti ngati—ngati Yesu akanati awapatse iwo mpumulo,* tsiku lopuma, *ndiye sibwenzi iye* pambuyo *pake atayankhula za tsiku lina.*

161 Pamene Iye anasintha lamulo, kuchokera ku lamulo kupita ku chisomo, kodi Iye sakanakhoza kuwapatsa iwo tsiku kuti apumule, tsiku lopuma, tsiku linalake? Koma Iye sanayankhule kanthu za sabata. Iye sanayankhule kanthu za Lamlungu, Iye sanayankhule kanthu za Loweruka. Koma pano pali chimene Iye adanena, Paulo anati. Tsopano penyani, "Apo . . . " Ya 19 . . . kapena ndime ya 9:

> *Apo patsalira chotero* sabata *kwa anthu a Mulungu.* (Ndilo lero!) . . . *Apo* patsalira . . . sabata *kwa anthu a Mulungu.*

Pakuti iye (inu kapena ine) yemwe *walowa mu mpumulo Wake* (Mpumulo wa Yesu, "Bwerani kwa Ine, nonse inu amene mwavutika ndi kulemedwa nao akatundu, Ine ndidzakupatsani inu Mpumulo"), *iye* (inu kapena ine) *watsiriza ku* ntchito *yake yomwe, monga Mulungu anachitira ku yake* pachiyambi.

162 Ameni! Ndi iyo sabata yanu. Ndi kulondola uko?

Tiyeni ife tivutikire. . . (anatero Paulo). . . *kuti tilowe mu mpumulo umenewo, mwina munthu wina aliyense angagwe potsatira chitsanzo chomwecho cha kusakhulupirira* (kwa masiku ndi zina zotero, mwaona).

Pakuti Mawu a Mulungu ndi achangu, ndi amphamvu, ndi akuthwa kuposa lupanga lakuwiri lirilonse, lopyoza ngakhale. . . *kugawa molekanitsa solo*. . . ndi *ozindikira za*. . . *ndi za*. . . (tiyeni tiwone). . . za *mzimu, ndi za*. . . (miniti yokha). . . *kulekanitsa kwa solo ndi mzimu, ndi*. . . *molumikiza ndi mafuta a mmafupa, ndi*. . . *ozindikira za mmaganizo ndi zolinga za mumtima*.

Palibe ngakhale cholengedwa chirichonse. . . *chiri* chosaoneka *pamaso pake: pakuti zinthu zonse ziri zamariseche ndi* zovundukulidwa patsogolo pa diso Lake *la iye yemwe ife tiyenera kuchita naye*.

163 Tsopano, penyani, Mulungu anapuma tsiku lachisanu ndi chiwiri, analilenga tsiku lachisanu ndi chiwiri, analipereka ilo kwa Ayuda ngati chikumbutso. Ine ndikuyankhula za Paulo Woyera tsopano, mwaona. Apa Izi. . . Tsopano, inu mukuganiza iye anali kuchibweretsa Icho? Kodi inu mukuganiza iye anali nao ufulu? Tsopano, kodi iye ananena chiani mu Agalatia 1:8? "Ngati mngelo wochokera kumwamba akanati adze nadzakuphunzitsani inu Uthenga wina uliwonse wosiyana ndi umene ine ndaunena, msiyeni iye akhale kwa inu wotembereredwa." Onani, mauthenga ali achimvekere. Tsopano, penyani.

164 "Chabwino, M'bale Branham, tsopano ine ndikadachita chiani kungokhulupirira Yesu Khristu?" Ayi. Uwo Sindiwo Mpumulo.

165 Tsopano, ngati inu mukufuna kuti mudziwe chomwe. . . Ndi angati akufuna kuti adziwe chomwe Mpumulo wa Chikhristu uli, nenani "Ameni." [Osonkhana ati, "Ameni!"—Mkonzi.] Tsopano, inu mukhoza kuzilemba izo ngati inu mukufuna kutero, Yesaya 28. Iye anati, "Langizo liyenera likhale pa langizo—langizo", akuyankhula. "Langizo pa langizo, mzere pa mzere, kuno pang'ono ndi uko pang'ono, ndipo mugwire zolimba ku icho chomwe chiri chabwino." Mneneri akuyankhula za nthawi ili nkudza, za Mpumulo, sabata. Muwerenge mutu wonsewo, muone, iye akuti, "Nthawi kumeneko pamene tsiku la sabata liti lidzathetsedwe," ndipo iwo azidzagulitsa nsapato

Loweruka mofanana monga iwo ankachitira izo Lolemba, kapena chirichonse chowonjezera. Inu mukuona? Anati, "Kodi nthawi iyi idzakhalapo liti?" Anati:

> *. . . langizo pa langizo; . . . mzere pa mzere; kuno pang'ono, ndi uko pang'ono: gwira zolimba ku chimene chiri chabwino.*
>
> *Pakuti ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena ine ndidzayankhula kwa anthu awa.*
>
> . . . Ndipo *ili ndilo* sabata, *mpumulo* umene ine ndinati iwo ayenera kuti alowemo. Ndipo mwa za izi zonse iwo anaumitsa mitima yawo ndipo anagwedeza mitu yawo ndipo anaukana Iwo. (Basi chinthu chomwecho iwo anachichita pa Pentekoste pamene Mzimu Woyera unagwera pa anthu, ndipo Mzimu Woyera unaperekedwa koyamba kwa anthu kumbuyo uko pa Tsiku la Pentekoste. Umenewo ndiwo Mpumulo, sabata kwa anthu a Mulungu.) . . .

166 Chotero chifukwa chokha chimene ife timasungira Lamlungu, zinayambika ndi atate athu amakezana a Baibulo, Paulo Woyera, Yohane, Mateyu, Marko, Luka, ndi onse awo, iwo ankapita nyumba ndi nyumba, iwo ankatenga mgonero pa tsiku loyamba la sabata pamene ophunzira amadza palimodzi, ndipo ilo linkatchedwa, osati sabata, koma tsiku la Ambuye.

167 Yohane anati, pa Chisumbu cha Patmo, nkuti atakhazikitsidwa kale movemerezeka mu mpingo, "Ine ndinali mu Mzimu pa tsiku la Ambuye." Ndiko kulondola. Mwaona? Ndiyeno iye anaona . . .

168 Ndipo—ndipo, tsopano, tsiku la Ambuye ndilo—ndilo tsiku limene Ambuye anauka. Tsopano, inu mupite mukawatenge wazambiriyakale, Josephus, Actibus [Kalembedwe kosatsimikizika—Mkonzi.], ambiri a ena awo. Kapena osati Actibus, o, ine sindingakhoze . . . Aliyense wa olemba achikale awo, ndipo inu mukazipeza kumbuyo uko. Azambiriyakale a mpingo, *Bukhu la Foxe la Ofera*, ndi ena ambiri, ndipo inu mukapeza mmenemo kuti kusiyana kokha . . . Iwo ndi gulu la Ayuda. Ena a iwo ankawatcha "odyana" amenewo anali Akhristu. Iwo ankati, "Uko kunali munthu yemwe Pontius Pilato anamupha ndipo ophunzira anabwera ndipo anadzaliba thupi Lake. Ndipo iwo anakalibisa ilo, ndipo lirilonse—Lamlungu lirilonse iwo ankapita kukadyako gawo la ilo." Iwo anali kutenga mgonero, inu mukuona. Iwo basi . . . Iwo anali kudya thupi Lake, inu mukuona. Iwo ankati iwo anali akudya thupi la Ambuye, mgonero. Ndipo iwo sankadziwa chomwe icho chinali, ndipo iye anati, "Iwo anali odyana." Anati, "Iwo amapita kukalidya pa tsiku loyamba la sabata, iwo amakumana pamodzi ndi kumadya thupi la munthu uyu."

169 Ndipo njira yokha yomwe iwe ungadziwire kaya iwo anali osunga-lamulo ndi okana mowawitsa chiukitsiro, kapena kaya iwo anali Akhristu ndi okhulupirira chiukitsiro, wina ankapita ku tchalitchi Loweruka ndipo wina ankapita ku tchalitchi Lamlungu, chimene chinali chizindikiritso pakati pa iwo.

170 Izo ndi zolimba kwambiri, si choncho izo? Chabwino. Ndikuyembekeza izo zikuchigwira icho. Mzimu Woyera uli . . .

171 Tsopano, inu muli ndi chinachake apo, m'bale? Inu mukufuna . . . Kodi inu mukufuna—kodi inu mukufuna kuti mukwere ndi kudzaliyankha ilo? Tiyeni tiwone, pomwe pano. O, inde.

5. Kodi Ayuda adzakhala nawobe mwayi kuti apulumutsidwe itatha nyengo ya Amitundu kufika kumapeto?

172 O, mayi, ngati ilo siliri lokongola! Ife tiribe nthawi yoti tipite mu ilo mwabwino kwenikweni, koma ndiroleni ine ndikuuzeni inu izi. Ndipo inu mutenge mau anga ine ndikuonetsani inu. Mwa . . . Ngati inu muti mutenge Mawu anga (momwe ine ndikuwafotokozera iwo) kwa Mulungu, ndiye inu mupite mukachiyang'ane icho, mwaona, ndiye inu mukapeza. Chifukwa ine ndikulingalira . . . Ine sindikutha kuiwona koloko, koma ine ndikulingirira iyo yapitirira . . . Kodi ndi nthawi yanji iyo? Chiani? Hafu pasiti naini. Ine ndiri kuyenera kuti ndipite ku chipatala panobe, ndipo ndiyenera kuti ndipite ku New Albany panobe, ndipo ife tiyenera kukhala tikutuluka pa twente faifi pasiti firii mmawa. Chotero . . . Ndipo ine ndakhala ndisakupita kukagona isanakwane thuu kapena firii koloko usiku uliwonse sabata ino.

173 Tsopano zindikirani pano, mwamsanga tsopano, kuti titenge izi. Inde, bwenzi langa la Chikhristu lokondedwa, tsiku la Amitundu latha, likutsirizika pakali pano. Ndipo Mulungu adzabwerera kwa Myuda. Ndipo mundirole ine ndinene kwa mpingo wawung'ono uwu umene ine ndimawupempherera mosalekeza. Ndi maulosi ochokera ku madera osiyana a dzikoli, akutsanulira munomo okhudza izi. Ine ndikukhulupirira kuti Myuda . . . Tsopano, valanibe zikhoto zanu miniti yokha, tsopano.

174 Myuda sanayambe wakhoza kuchilandira chinthu chimodzi ichi cha mpingo wa Chikhristu. Myuda wandiuzapo ine, nthawi zambiri, "M'bale, inu simungakhoze kumudula Mulungu mu zidutswa zitatu ndi kumupereka Iye kwa ine." Myuda ali ndi Mulungu mmodzi, ndipo uyo ndi Yehova.

175 Ndipo Wamitundu wazipotoza izo mochuluka kwambiri, mpaka iye waziphunzitsa izo mwanjira ina, komabe, ndi chidziwitso. Ine ndikhulupirira iye—iye ali ndi lingaliro—lingaliro la icho, kuti kulibe amulungu atatu. Kuli Mulungu mmodzi, maonekedwe atatu. Umunthu utatu mwa Munthu mmodzi. Ndipo pamene inu mungaumvetse uthenga,

ine ndinanena kwa Hyman Appleman . . . Ambiri a inu mumamudziwa iye. Iye anati, "M'bale Branham, ngati inu muti muutengere uthenga umenewo ku Palestina ndi zizindikiro ndi zodabwitsa," anati, "kukakhala Ayuda milioni ati akamulandire Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wawo." Mwaona, ndiko kulondola. Tsopano, ine ndinati . . .

176 Pano pali Uthenga umene ife tiri nao panowu. Yesu anali Yehova ataphimbidwa mu thupi, anabwera pansi anaphimbidwa. Tsopano, Mulungu (Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera) sali monga chala chanu, mmodzi, monga anthu ena amaganizira izo. Chinthu chonsecho changokhala monga . . . Ayi, Mulungu ndi . . . Ine ndinangofutukulira icho kwa inu kanthawi kapitako, mwaona, kuti pali utatu mwa Mmodziyo.

177 Ine ndine utatu mwa mmodzi. Ine ndine solo, thupi, ndi mzimu mwa munthu mmodzi. Ndi kulondola uko? Zedi. Ine ndiri—ine ndiri wopangidwa ndi—ndi timakhungu, magazi, ndi mitsempha, ndipo komabe ndiripo mmodzi. Mwaona? Chirichonse chimene inu mumachiyang'ana chiri mu utatu, ndipo utatuwo uli mu chimodzi.

178 Munali utatu mu chombo. Phaka lapansi, zinthu zokwawa; phaka lachiwiri la mbalame, zinthu zouluka; ndipo phaka lachitatu la Nowa ndi banja lake. Chirichonse!

179 Mu kachisi. Munali kosonkhana, malo opatulika, Opatulika Mopatulikitsitsa. Mwaona?

180 Ndipo pakhala pali nyengo zitatu. Yautate, Yaumwana, ndi nyengo ya Mzimu Woyera. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Koma zitatu zonse izo . . . Ife sitimanena kuti, "Amulungu athu." Icho ndi chikunja, ndipo Myuda amazidziwa izo. Koma pamene inu mungathe kuzipangira izo kwa iye kuti Yesu uyu ALI Mulungu, Yehova Mulungu, osati munthu wachiwiri kapena munthu wachitatu, ndi Munthu yemweyo nthawi zonse kudzipanga Yekha kuonekera. Mwaona? Ndiyeno ndi zizindikiro ndi zodabwitsa kuti atsimikizire kuti Yesu wauka kwa akufa.

181 Ndipo Dokotala Reedhead uyu . . .

182 M'bale kumbuyo uko, mphunzitsi wa mpingo . . . mphunzitsi pa . . . mphunzitsi wa sukulu, muno mu tchalitchi usikuuno, ine ndinamuwona iye, ndipo ine ndinagwirana chanza ndi mkazi wake ndi khanda kumbuyo uko. Iye anali kunja uko kuti ndikamumvere iye akulalikira usiku wina. Ine ndikuganiza iwo ali pano, ngati iwo sanapite, ndikukhulupirira iye ndi mphunzitsi wa sukulu mu Louisville. Mulimonse, iwo anapita kunja uko kuti akamumvere iye.

183 Ndi zopambana, mwamunayo anabwera ku nyumba kwanga, iye ndi wina (ndi Myuda), miyezi ingapo yapitayo. Ndipo iye anati, "M'bale Branham, ine ndiri nawo madigirii *ochuluka kwambiri* ochokera ku Bob Jones. Ine ndiri . . . ochokera ku

Wheaton." Maphunziro onse omwe akadaunjikidwa kwa iye! Anati, "Ine ndakhulupirira Mulungu kuyambira ine ndiri mnyamata wamng'ono." Ndipo anati, "Komabe moyo wanga uli wopandamo kanthu!" Iye anati, "Kodi aziphunzitsi akhala akulakwitsa?"

184 Ndipo pano pali chovomereza. Ngati wina . . . Ngati ena a inu munali uko ku Open Door usiku wina, pamene ife tinalipo apang'ono tikulalikira limodzi. Iye anati, "Pamene ine ndiri ndi chonena changa . . ." Tsopano, mvetserani, kachisi wamng'ono, chifukwa cha mapemphero anu ndi zinthu zomwe zathandizirapo, mvetserani ku ichi. Iye anandiuza ine izo kale, kuno ku nyumba.

185 Iye anabwera ku nyumba kwanga, iye anati, "M'bale Branham," anati, "Ine ndakhala ndiri kakasi." Iye anati, "Kodi pali chinachake chachikulupo kuposa ichi chomwe ine ndachikhulupirira ndi kuchilandira, Khristu monga Mpulumutsi wangawanga? Ndipo ine ndikukhulupirira kuti ine ndiri obadwa kachiwiri mwa Mzimu, koma ine ndiribe umboni wa chirichonse."

186 Ine ndinati, "M'bale, moipa monga ine ndikuchida kuti ndinene icho, aziphunzitsi akunyengani inu, kuphunzira kwanu."

187 Penyani, monga ine—ine ndikhoza kunena izo, ine sindimakhulupirira mu kuimika matola pa njira yanu ya Kumwamba: "Kodi inu mumakhulupirira izi?" mu mipingo, "Tsopano, umu, mundilole ine ndifunefune umu, b—Baibolo limanena *izi*, kodi inu mumazikhulupirira izo?" Mdierekezi amakhulupirira ndipo amanjenjemera! Si chimene iwe umachikhulupirira. Mzimu wako umayenera kukhala ndi umboni ndi Mzimu Wake kuti ndinu ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, pa kukhala obadwa kachiwiri ndipo mutalandira ubatizo wa Mzimu Woyera.

188 Iye anati, "M'bale Branham, inu mukuganiza chiani za Achipentekoste?"

189 Ndipo ine ndinati, "Ndi chifukwa ine ndikuchita nawo. Ndi chifukwa ine ndiri—ine ndikupusitsana ndi iwo, iwo ali nacho chinachake chimene inu mulibe." Ine ndinati, "Ndi zongotengeka zao ndi zirizonse, iwo ali ndi choonadi chimene inu simudziwa kanthu za icho." Ndipo ine ndinali kuyankhula kwa mmodzi wa anthu akulu kwambiri mu Amereka, pomwepo. Inde, bwana. Iyeyo ndi Purezidenti wa Mamishoni aku Sudan, ndi wamkulukulu mdziko lonse, wachikhazikitso mpaka pachirikati. Iye ankawadziwa Malemba, ndi *imfa*, *kuikidwa* ndi *chiukitsiro*, kumangozilalikira izo monga nyumba ikuyaka. Koma izo si Icho. Mdierekezi akhoza kuchita izo, nayenso. Mdierekezi ali wachikhazikitso basi monga iye angakhoze kukhalira.

190 Koma, m'bale, Yesu Khristu anati, "Kupatula munthu akhale atabadwa mwa Mzimu wa Mulungu iye sadzauona Ufumu wa Mulungu."

191 Osati basi chifukwa inu mukuti, "Inde, ine ndikukhulupirira izo. Eya, ine—ine ndikukhulupirira kuti izo ziri chomwechodi. Ine ndikukhulupirira izo. Inde." Izo sizimachita icho ayi. Icho chiyenera kuti chikhale chochitika chenichenicho cha Kubadwa mwatsopano. Icho chiyenera kukhala chinachake pakati pa iwe ndi Mulungu choti iwe ukudziwa kuti wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo.

192 Anati, "M'bale Branham, kodi ine ndingakhoze kuulandira Mzimu Woyera?"

193 Ine ndinati, "Ndangoika kumene manja pa Hyman Aplleman kumusi uko, ndipo iye waulandira ubatizo wa Mzimu Woyera."

194 Myuda wina uyu anayamba kulira, ndipo anaswa chikho pa gome la khofi apo, ndipo analira kwakukulu mwaching'ang'adza cha pamenepo. Awiri onse a iwo anati, "M'bale Branham, kodi ife tingalandire chotani Mzimu Woyera?" Masikolala! Akuthwa zedi, ochenjera! Opambana omwe alipo mu dzikomu!

195 Ndipo ine ndinati, "Njira ya utumwi ya kulandirira Mzimu Woyera ndiyo kuika manja pa iwo." Ndiko kulondola.

196 "Kuika kwa manja." Anania anadza nadzaika manja pa Paulo kuti iye akhoze kulandira kupenya kwake ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera.

197 Filipo anapita kumeneko ndipo anakalalikira kumeneko, ndipo analibatiza gulu lonselo kumeneko mu Dzina la Yesu Khristu. Mzimu Woyera unali usanadze pa aliyense, chifukwa Petro anali ndi mafungulo. Ndipo iye anadza uko, ndipo iye anaika manja pa iwo, ndipo iwo analandira Mzimu Woyera. Ndi kulondola uko?

198 Paulo, mu Machitidwe 19, iye atadutsa uko. Apolo, anali Billy Graham choimira kumtunda uko, anali ndi chitsitsimutso chachikulu ndi nthawi yabwino. Iye anati, "Kodi inu munalandira Mzimu Woyera chiyambire pamene munakhulupirira?" kwa gulu lija la Abaptisti.

199 Iwo anati, "Ndife otsatira a Yohane. Ife tikudziwa! Apolo ndi mlaliki wathu, iye ndi wa zamalamulo wotembenuka, munthu wanzeru kwambiri mu dzikoli."

200 Iye anati, "Koma kodi inu munalandira Mzimu Woyera chiyambire pamene munakhulupirira?"

Iye anati, "Ife sitikudziwa ngati kuli Mzimu Woyera uliwonse."

Anati, "Ndiye inu munabatizidwa motani?"

Anati, "Ife tinabatizidwira kwa Yohane."

201 Anati, “Iye ankabatizira kwa kulapa, kumanena kuti inu mukhulupirire pa Iye ati adzeyo, pa Yesu Khristu.” Ndipo pamene iwo anamva Ichi iwo anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo Paulo anaika manja ake pa iwo ndipo iwo analandira Mzimu Woyera, anayamba kumayankhula mu malirime ndi kumamukuza Mulungu. Izo ziri momveka monga ine ndikulidziwira Lemba.

202 Tsopano, penya, mzanga! Pakhoza kukhala pali kusiyana pang’ono apa mu malingaliro anu, chifukwa ife tasokonezeka ndi chirichonse. Koma tiyeni tichiyale icho apa, osati kuyesa kuikapo tanthauzo lanu. Muzinena chomwe Baibuloli limanena, ingochiwerengani Icho momwemu.

203 Ndipo ine ndinati, “Chinthu chokha ine ndikuchidziwa, abale, ndi kuika manja pa iwo amene akufunafuna Mzimu Woyera.”

204 Iye anati, “Kodi inu mungatiike manja ndi—ndi kumfunsa Mulungu kuti atidalitse ife ndi kutipatsa ife Mzimu Woyera?”

205 Ine ndinati, “Ine nditero.” Ndipo ife tinagwada pansi, ndipo ine ndinapemphera ndipo ndinaika manja pa iwo. Ndipo pafupi masabata pang’ono zitachitika izo, onse a iwo analandira ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo pamene Dokotala Reedhead uyu analandira ubatizo wa Mzimu Woyera, anabwera akuyankhula mu malirime ena. Inde, bwana.

206 Ndipo Mamishoni aku Sudan anu anati, “Ife tiribe malo kwa munthu yemwe angayankhule mu malirime.”

207 Ndipo iye anadza kwa ine ndipo anati, “ ‘Winawake kumayankhula mu malirime’?”

208 “Bwanji, bwanji,” ine ndinati, “iwo alibe malo kwa Yesu Khristu, chifukwa Yesu Khristu anayankhula mu malirime osadziwika; ndipo anafa, akuyankhula mu malirime osadziwika.”

209 Iwo sakanakhoza kuvomereza chiphunzitso cha Paulo, Paulo ankayankhula ndi malirime kuposa ena onsewo.

210 Wina anati kwa ine dzulo, anati, “Ine kuli bwino ndiyankhule mau asanu ndi kumvetsa.”

211 Koma chiphunzitso cha Paulo chinati, “Khumbani ulosi, ndipo musamaletse kuyankhula ndi malirime.” Ndipo iwo amaletsedwa kuyankhula ndi malirime!

212 Kuyankhula mu malirime ndi mphatso Yauzimu ya Mulungu yomwe ili ya mu mpingo mofanana basi lero monga iyo inali kumbuyo uko pachiyambi. Ndicho ndendende Choonadi. Inde, indedi! Ndicho chiphunzitso cha Baibulo. Iyo ndi mphatso Yauzimu, ndipo inu mumaikana iyo mofanana basi monga inu—inu mumakanira Kubadwa kwatsopano, inu mumakana chirichonse chimene Yesu ankaphunzitsa pamene inu muyesa kuzidulira izo kunja.

213 Tsopano, inu mukhoza kulusa pa izo, ambiri a iwo atero. Koma ine ndikuti, "Icho chiri ndi malo ake." Icho chiri monga ngati peyala ya nsapato; pamene inu mugula peyala ya nsapato, malirime amakhala mmenemo. Ndipo uko nkulondola. Pamene inu muli mkati mwa Thupi la Khristu, Mulungu amakhala ndi gome lonse lokonzedwa modzadza, pano. Iye ali ndi chikondi, Iye ali ndi chimwemwe.

214 Ngati ine ndikanapita ku gome lanu ndi kukhala pansi pamenepo, ndipo inu nkuti, "Mlaliki, bwerani mudzadye ndi ine," ine ndikanakhulupirira inu mumandikonda ine. Ndipo inu mukanakhala ndi nyemba ndi mbatata ndi makaroti ndi nkhuku yokazingidwa ndi chitumbuwa cha dzungu ndi ayesikirimu, chirichonse chiri pamenepo. Bwanji, ine ndikhulupirira ine ndikadakhala basi ngati wolandiridwa ku mbatata monga ine ndiri ku nyembazo. Chinthu chokha, ine ndikukhulupirira ine nkadakhala woti ndalandiridwa ku nkhuku monga ine ndinali ku chitumbuwacho. Izo zonse ziri pa gomepo. Ndipo chinthu chokha ine ndinayenera kuchichita ndi kuti, "Chonde ndipatsireni ine zitumbuwa zina?" Ndipo ine ndikukhulupirira ndi mtima wabwino womasuka, mchikondi chanu kwa ine, inu mukanati, "Ndithudi, m'bale wanga, kwayani chidutswa chabwino chachikulu cha izo." Ndi kulondola uko? Ngati ine ndikanati, "Kodi inu mungandipatsireko ine mbatata?" "Bwanji, ndithudi, m'bale wanga, ndi izi apa."

215 Ndipo dalitso lirilonse lachiombolo limene Yesu Khristu analifera naligula mu chitetezero Chake pa Gologota, liri litaikidwa pa gome ndipo wokhulupirira aliyense wakhala pamaso pake. Aleluya! Ngati ine ndikusowa machiritso, ine ndingangoti, "Atate, ndipatseniko ine machiritso ena," ndipo ine nkuwatsanulira iwo pa mbale yanga ndi kudya zazikulu . . . Tsopano, ngati inu mukufuna kufa ndi njala pitirirani nazo. Inde, bwana. Ndipo ulosi, kuyankhula mu malirime . . .

216 Ndipo—ndiyeno munthu analemba umoyo, iye sankadziwa kuti ine ndinayankhula . . . ndinali nditayankhula ndi malirime mwiniwanga. Ndipo iye akulemba bukhu ili, inu mudzalipeza ilo lidzamwaza mafuko. Ndipo pambali pa izo, mwamuna uyu ali ndi alaliki otchuka makumi awiri ndi asanu a Sukulu ya Baibulo ya Moody omwe akufunafuna mphatso ya kuyankhula mu malirime. Anthu achikhazikitso asandulizika chadodolido. *Christian Life*, m—mwezi uno, tayang'anani pa magazini ya *Christian Life* mwezi uno, pa tsamba la naintini, ndipo mukayang'ane pa dokotala wamkulu uja wa zauzimu, anati, "Kodi ife tizilandire izi? Kodi ife tataya chinachake?"

217 Ine ndikuimva mvula yochuluka ikubwera! Inu muli ndi anthu akuchipotozera icho cha ku ngodya, koma icho chafika pa malo akuti Mulungu akulipatsa dziko la Amitundu kugwedeza ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, kuwutsanulira Iwo ndi chidzalo chake chonse ndi mphamvu ndi zizindikiro ndi zodabwitsa.

Chifukwa chomwe ine ndikugwira . . . Achipentekoste akhala akunkhidwira kunja pa ngodya ndipo apita molusa pa zinthu zosiyana monga choncho, nthawi inali isanache apobe. Ndicho chifukwa chake iwo akhala nazo zotentheka zonse izi. Koma ndilo lonjezo Lauzimu la Mulungu ndi Mawu Auzimu a Mulungu, ndipo Iwo ayenera kudza pokwaniritsidwa chifukwa Mulungu wanena kale choncho. Ndipo ine ndikukhulupirira basi kusanafike kutha kwa nyengo ya Amitundu kuti Mulungu adzatsawanulira achikhazikitso.

218 Inu mukhoza kuwerenga izo mu *Reader's Digest* ya mwezi uno, nkhani ya Ogasiti uno ya izo. Pitani kayang'aneni pa iyo, momwe kuti mlaliki wa Chimethodisti uyo kumusi uko mu guwalo uko, akumupempherera mwamuna uyo chigonere pamenepo kumafa pa kama wa chipatala, ndipo umboni wa Mzimu Woyera nkudza ndipo munthuyo anachiritsidwa pomwepo. Aleluya! Zedi. Mulungu ali nawo machiritso Auzimu ali pa gome pano! Iye ali ndi ulosi uli pa gome pano! Iye ali nako kuyankhula mu malirime pa gome pano! Iye ali nazo mphatso zauzimu zisanu ndi zinai mu Thupilo, ndipo ndinu olandiridwa ku iliyonse ya izo! Aleluya! Inde, bwana, ife tiri pano.

Kodi . . . Pa kutsekera kwa Amitundu, Kodi Ayuda adzabwezedwa?

219 Inde, bwana. Malemba ambiri, mlongo, m'bale, yense yemwe iye ali. Yoweli mwa mmodzi, "Chimene chimbalanga chinasiya, achirimamine anachidya," ndi zina zotero, mtengo uja. Ndipo Yesu anatero Iyemwini momwe iwo akanati adzabwezedwe ndi chirichonse. O, Lemba lonselo, Daniele ndi paliponse, akuyankhula za izo. Inde, Yesu anati, "Pamene inu mudzawona mtengo wa mkuyu ukuphukira masamba ake, dziwani kuti nthawi ili pafupi."

Ine ndikukhulupirira limzake limodzi ili likuchita chinachake ndi izo.

6. Kodi inu mukukhulupirira kuti Ayuda—Ayuda kubwerera ku Palestina ndi kukwaniritsidwa kwa ulosi wa Baibulo? Ife tamva kuti inu mumapita ku Palestina, kodi izo nzoona?

220 Inde. Inde, bwana. Mundirole ine ndikuuzeni inu chinachake, chimodzi mwa zazikulukulu . . . Ngati inu mukufuna kuona nthawi ya chaka yomwe ili, muyang'ane pa kalendara. Ngati inu mukufuna kuona nthawi ya usiku yomwe ili, muyang'ane pa koloko. Ngati inu mukufuna kuona tsiku lomwe inu muli kukhalamo, muyang'ane kumene Ayuda ali. Ndiwo choonera nthawi cha Mulungu.

221 Ndipo tayang'anani! Usiku womwewo, tsiku lomwelo, limene mngelo wa Ambuye anakomana nane, 1946, pa Meyi seveni, ku Chigayo cha a Green, Indiana, tsiku lomwelo chikalata cha mtendere chinasainidwira kwa Ayuda ndipo iwo

anali fuko lokhazikitsidwa kwa nthawi yoyamba kwa zaka twente-faifi handiredi. Aleluya!

222 Ndipo, usikuuno, mbendera yakalekale mu dziko lonse, nyenyezi ya mivi isanu ndi umodzi ya Davide, ili petupetu pa Yerusalemu kwa nthawi yoyamba mu zaka twente faifi handiredi, kuchokera pakutengedwa kutali kupita ku Babeloni. Yesu anati, "Pamene inu mudzaona mtengo wamkuyu ukuphukira masamba ake." Ndi uyo uko! Pamenepo Iye anati, "Phunzirani fanizo. Inu mumati 'dzinja layandikira.' Pamene inu muona izi, dziwani kuti nthawi ili pa khomo." Ife tiri kumene pa mapeto a nthawi.

223 Onani momwe "chonyansa" cha Daniele, ndi zina zotero, inu mukudziwa, pamene Yesu ananena. "Pamene Karonga wamkulu adzabwera, Iye adzanenera—masiku sauzande ndi thuu handiredi ndi sikisite," zomwe zinali zaka zitatu ndi miyezi isanu ndi umodzi. Ndipo izo ziri ndendende zimene Yesu analalikira. Iye anabwera kwa Ayuda okha, ndiye Iye akanadzadulidwa kukhala—nsembe kwa anthu. "Ndipo chonyansa chimenecho chopangitsa chipululutso," Achimuhamadi anaimika Chisilamu cha Omar kumeneko. "Ndipo iwo akanati adzapondereze pansi makoma a Yerusalemu mpaka" (fyuu! Mpaka chiani?) "nyengo ya Amitundu ikhale itakwaniritsidwa." Ndiyeno Iye adzabwerera kwa Ayuda kachiwiri, ndipo apo ndi pamene Nkhondo ya Armagedoni ikuchitika . . . Pamenepo Iye anawaitana Amitundu, kuti atulutse anthu kwa Dzina lake, Mkwatibwi Wake. Zindikirani. Inde, bwana. Handiredi ndi forte-foro sauzande ali onse Ayuda owomboledwa amene ayenera kuti adzayime pamenepobe. Onse awa . . .

224 Ndiye pamene Mpingo watengedwera mmwamba, Mose ndi Eliya akuwonekera, mu Chivumbulutso 11, ndipo akulalikira Yesu Khristu kwa iwo. Ndipo Mzimu Woyera ukutengedwa kuchokera kwa Amitundu, ndipo Mkwatulo ukudza kuti Mpingo utengedwere mmwamba. Ndipo Ayuda amene asiyidwa kuno adzalalikiridwa kwa zaka zitatu ndi theka, chifukwa iye anati, "Pali Masabata sevente akadali otsimikiziridwa pa anthu Ako, ndipo Mesiya adzadulidwa kwenikweni pakati pa iwo." Pamene Iye akuchotsedwapo, Amitundu adzapatsidwa malo, ndiyeno iwo ali nazo zaka zitatu zina ndi theka kuti alalikiridwe, za Yesu Khristu.

225 Zedi, Ayuda akubwera. Ndipo ine ndikukhulupirira, m'bale, kuti pamene ife tikafika uko ku Palestina nthawi ino . . . O, pempherani! Iwo akuwerenga Baibulo limenelo.

226 Mfundo imodzi yokha yowonjezera, ndiye ine ndiri ndi funso laling'ono, lalifupi pano, ndipo ndiwo onse a iwo. Limodzi ili pano ine ndikuganiza ndi pemphero.

227 Tayang'anani pa ichi! Dokotala Reedhead anati, ataimirira apo akuyankhula kwa wa Chimuhamadi wophunzira . . .

228 Tsopano, ikani makutu anu mmwamba mwatcheru. Wa Chimuhamadi, ine ndinali nawo twente sauzande a iwo anadza kwa Ambuye Yesu pamene iwo anaona zizindikiro ndi zodabwitsa uko mu Afrika. Ichi . . . Kapena, ayi, osati twente sauzande; ndi sate sauzande mwa onse. Ine ndikuganiza iwo anali teni sauzande a iwo anadza, pakuti unyinji waukulu unali—unali Achimuhamadi. Ndipo pamene iwo anaima pamenepo, ndipo ine ndinati, "Ndi ndani mmodzi wa aneneri anu ku kachisi angakhoze kumupangitsa mwamuna uyu kuchira?" Ine ndinati, "Ndi liti mwa mafano anu, kwa inu mbadwa, lingakhoze kumupangitsa munthu uyu kuchira?" Ine ndinati, "Palibe mmodzi wa iwo! Palibe mneneri ku kachisi . . . ndipo palibe wansembe, kani." Ndipo ine ndinati, "Palibe fano lingakhoze kuchita izo. Ndipo ngakhalenso ine sindingathe. Koma Mulungu wa Kumwamba wamuukitsa Mwana Wake Yesu Khristu Yemwe ali wamoyo pakati pa anthu lero, Yemwe wamupanga iye kuchira mwangwiro monga inu mukumuonera iye ataima." Munthu ali ndi unyolo kuzungulira khosi lake, amachita kumutsogolera iye ngati galu. Mu nthawi ya miniti imodzi anali ataimirira pa mapazi ake, wolunga ndi wabwino.

229 Ndipo Dokotala Readhead anandiuza ine usiku wina pamene ife tinali titakhala uko mu galimoto, iye anati, "O, mai!" tikuganizira za izo. Iye anati wa Chimuhamadi uyu anabwera kwa iye, ndipo anati iye anali kuyankhula ndi wa Chimuhamadi uyu, munthu wophunzira kwambiri. Iye anati, "Chabwino, bwana, bwanji inu osamukana mneneri wanu wakale wakufayo, Muhamadi?"

230 Tsopano, kumbukirani, Achimuhamadi amakhulupirira mwa Mulungu. Kunja uko mu—mu Afrika, "belu" lalikulu, "pansanja," limapachikika mmwamba monga choncho. Ndipo iwo amatenga nyundo yaikulu kwambiri ya chimpira ndi kumalimenya ilo monga choncho, ndipo ilo limalira ponseponse mu dzikolo. Ndipo wa Chimuhamadi aliyense amaima, ndipo wansembe amatuluka pamwamba pa kachisi, ndi kuti, "Pali Mulungu mmodzi woona ndi wamoyo, ndipo Muhamadi ndiye mneneri Wake."

231 Awo ndi ana a Ishimaeli. Mwaona, Hagara, iwo ndi ana a Abrahamu kuchokera mwa Hagara. Mwaona? Iwo amakhulupirira mwa Yehova Mulungu woona, koma iwo amaganiza kuti Yesu . . . (Uyo anali . . . Iye ndi Muomboli *wathu*, wotumizidwa kwa Amitundu kuchokera mwa mkazi waufulu; Isaki, mwaona, ndi kudzera mwa Sarah). Ndipo tsopano, iwo anali kupyolera mwa Hagara, Ishimaeli, ndipo kunadza Achimuhamadi.

232 Ndipo pa manda a Muhamadi, inu muyenera mupite mukaone, izo ndi zokhudza, manda aakuluwo kumeneko. Ndipo kwa zaka zikwi ziwiri apo pakhala pali kavalo woyera ataikidwa chisyalo, ataima pamenepo. Muhamadi analonjeza kuti iye

akanati adzauke kwa akufa tsiku lina ndi kudzalumphira pa kavalo ameneyo ndi kuligonjetsa dziko. Ndipo iliyonse—mphindi iliyonse iwo amangosintha kavalo mmodzi kwa mzake; kuyembekezera pamenepo ndi mlonda wokhulupirika, ataima, kuyembekezera Muhamadi kuti awuke kwa akufa. Zaka zikwi ziwiri zapita kuyambira apo.

233 Iwo amakhulupirira mwa Yesu, iwo anati Iye anali mneneri. Pa makoma za Yerusalemu wakaleyo pali chikachisi chachikulu kwambiri chomangidwa, chimene chiri cha Muhamadi kuti adzafikireko. Ndi ka kachisi kakang'ono kwambiri kumusi kuno, komwe kali ka Yesu. Mwaona, iwo anati, "Yesu sanapachikidwe, iwo onse anali atazisokoneza izo." Anati, "Iye anakwera pa kavalo ndipo anapita kwina." Mwaona? Tsopano, iwo—iwo amakhulupirira zimenezo.

234 Iwo ali ndi kadontho kofiira pakati pa maso awo. Anthu uko amene akupita ku India, inu mukakazindikira iko. Mai, iwo adzaima uko mwa zikwi.

235 Ndiyeno Dokotala Readhead anati iye anali ataimirira apo, ndipo iye anati, "Tsopano, bwanji inu simukusiya mneneri wakale wakufa uyo ndi kulandira Mmodzi Yemwe anauka kwa akufa, Khristu wamoyo?" Tsopano, iye anali sikolala ndipo iye ankadziwa momwe angawaikire mawu ake.

236 Anati wa Chimuhamadi anayang'ana pa iye, (wanzeru, mwamuna wophunzira, momwe muno mu Amereka, anali ataphunzitsidwa kuno) iye anati, "Bwana, bwana wachifundo, Yesu wanu woukitsidwayo angandichitire ine chiani choposera chomwe mneneri wanga wakufayu wachita?" Anati, "Mneneri wanga wakufa anandilonjeza ine Moyo pambuyo pa imfa. Ndi chomwe Yesu wanu anachita." Chabwino, iye anali ndi chinachake. Anati, "Tsopano, onse a iwo analemba bukhu. Inu mumakhulupirira ilo limene Yesu analilemba, ine ndimakhulupirira limene Muhamadi analemba. Iwo onse amalonjeza Moyo." Anati, "Kodi Yesu wanu angathe kuchita chiani chinanso kwa ine kuposa chimene Muhamadi wanga—wanga angakhoze?" Chabwino, mwamunayu, mu mfundo zophweka, icho ndi choonadi. Iye anati, "Koma mphindi yokha, bwana wachifundo." Iye anati, "Muhamadi wanga sanandilonjeze konse ine zinthu zonga Yesu wanu anachita. Yesu wanu analonjeza . . . Iwo anati, 'Iye anauka,' ndipo anati azikhala ndi inu nthawi zonse, mpaka kumapeto a dziko; ndipo zizindikiro zomwezo ndi zodabwitsa zomwe Iye ankachita, inu mukanati muzidzachita nanunso, mpaka kumalekezero a dziko. Inu mukanati muzichiritsa odwala, ndi kuukitsa akufa, ndi kuyeretsa akhate, ndi kutululutsa ziwanda." Anati, "Ine ndinaphunzira Chikhristu, bwinobwino." Anati, "Tsopano ndiloleni ine ndione inu aziphunzitsi mukuonetsera Yesu Khristu, ndipo ine ndikhulupirira kuti Iye anauka kwa akufa. Koma, kunja kwa icho . . . Muhamadi sanatilonjeze ife

konse zinthu zotero, iye anangotilonjeza ife Moyo pambuyo pa imfa. Ndipo icho ndi chinthu chomwecho chimene inu mumaphunzitsa, ndi kumachilambalala chinacho." Mwamunayo anali kulondola, wachimuhamadi anali kulondola ndendende.

237 Dokotala Readhead anati iye anaimirira ndipo analira. Anati, "M'bale Branham, ine ndinaganizira za inu." Ndipo iye anathamangira kuno, ndipo anapita mkati umo, ndipo ine ndinaika manja anga pa iye, ndipo ubatizo wa Mzimu Woyera unadza pa iye. Ndipo tsopano iye akumaona ngakhale masomphenya ndi chirichonse. Tsopano muloleni Wachimuhamadi akumane naye! Iye ndi munthu wosiyana!

238 Ine ndikuti Yesu wathu anauka kwa akufa, Iye ali moyo lero. Ndipo Iye akuchita zinthu zomwezo lero Iye ankazichita apo, mitundu yonse ya zizindikiro ndi zodabwitsa. Ndipo inu anthu achikhazikitso mwakhala mozungulira kumayesera kuti mufotokoze izo mopotoza, ndi kumaphonya gawo lachikhazikitso lomwe la Baibulo. Ndiko kulondola ndendende. Yesu Khristu, Mwana woukitsidwa wa Mulungu, akhoza kuyankhula ndi malirime ena kupyolera mwa inu, Iye akhoza kulosera kupyolera mwa inu, Iye akhoza kuonetsa masomphenya kupyolera mwa inu, Iye akhoza kutanthauzira zinenero zosadziwika kupyolera mwa inu. Ndipo zonse izo ziri gawo la Iye.

239 Ndipo kuti utenge gawo *ili* la Iye ndi kusiya gawo *ilo* kunja pa Iye, zikadakhala monga kundidula ine theka mu ziwiri ndi kutenga ziuno zanga ndi miyendo yanga mmusi ndi kuti inu mwanditenga ine, pamene gawo *ili* simuti mulilandire.

240 Inu mwina muyenera kundilandira ine mwathunthu... Ndipo ndicho chifukwa ine ndiri mlaliki wa Uthenga wathunthu amene amakhulupirira kuti chirichonse Mulungu anachinena ndi Choonadi. Ameni! Ulemerero! Ine ndikumverera monga woyera-wodzigudubuza pakali pano. Inde, bwana. Ine ndikukhulupirira Izo!

7. Mateyu 24:29, amayankhula za "Dzuwa kukhala litadetsedwa, mwezi sudzapereka kuwala kwake, ndipo nyenyezi zidzagwa kuchokera kumwamba." Kodi izi zidzachitika usanachitike kapena utachitika Mkwatulo, kapena Yesu atangotsala pang'ono kubwera kuti a-l-... alamulire pa dziko lapansi?

241 Mwa kukhulupirira kwanga kodzichepetsa, tsopano, ine sindikanati...Ine sindikudziwa, ine ndikuganiza iye akuyankhula za Mateyu 24, apo. Tsopano, Yesu akuyankhula za nyenyezi ndi zinthu kumagwa, ine ndikukhulupirira kuti izo ziri basi isanayambe nyengo ya Chisautso kukhazikika pa dziko lapansi.

242 Tsopano, ine ndiri ndi ganizo lachilendo kwenikweni apa limene ambiri a inu muti musagwirizane ndi ine pa ichi,

bwanji, ine ndikulingalira ena a nthawi zakale akundimva ndikuphunzitsa chomwe ife tinadutsa mwa icho. Onani, ine sindimakhulupirira Mpingo udzadutsa mu nyengo ya Chisautso. Ine ndikukhulupirira Mpingo udza . . . Onani, ine . . . Njira yokha ine ndimaphunzitsira Chipangano Chatsopano ndi mwa mthunzi wa Chipangano Chakale, basi monga Mzimu Woyera pano kwa tsiku la sabata ndi zina zotero. Chirichonse ndi mthunzi kumbuyo uko.

243 Tsopano, yang'anani kumbuyo mu Chipangano Chakale. Pamene inu muona miliri ikugwa, iwo anali mu Igupto. Sanali iwo? Ndipo Mulungu anali kuwatulutsa anthu Ake kupita ku dziko lolonjezedwa. Ndi kulondola uko? Ndipo Israeli sanalandire konse mliri umodzi. Basi pamene miliri . . . iwo usanapitepo, iwo anakalowa mu Gosheni. Ndi kulondola uko? Ndipo dzuwa silinachite mdima, palibe udzudzu unabwera, palibe achule anali kumeneko, palibe nsabwe inali kumeneko, palibe namondwe anali kumeneko, palibe mphezi inali kumeneko, palibe kuphedwa kwa ng'ombe kunali kumeneko, ndipo chirichonse iwo anali nacho chinali chitatetezedwa mu Gosheni. Ndi kulondola uko? Ndi choimira cha Mpingo ukupita basi isanayambe nyengo ya Chisautso. Yesu anati, "Pamene zinthu izi ziyamba kufika pochitika, mutukulire mmwamba mutu wanu, chiombolo chanu chayandikira." Mwaona?

244 Ine ndikukhulupirira kuti mwezi ndi dzuwa ndi nyenyezi . . . Ndiye iwo ananena kuti . . . Pitirira ndi kuziwerenga Izo, anati, "Ndipo anthu anathamanga ndipo anakadzibisa okha mu . . . ndipo anagwera pa iwo . . . anafuna kuti adziphe okha, ndipo sankakhoza kuchita izo, ndi chirichonse." Ine ndikukhulupirira izo zichitika basi chisanayambe Chisautso.

245 Tsopano, penyani, Chisautso chikudza. Pamene Chisautso chikantha, Mpingo ukupita mmwamba. Tsopano, kumbukirani, mpingo wamba chabe wopanda Mzimu Woyera ukudutsa kupyola nyengo ya Chisautso. Ndi osankhidwa okha amene akupitirira.

246 O, ine ndikanakhoza kukhula chinachake molimba apa, mwa miniti yokha. Kodi inu mungandipatse ine maminiti atatu ena? Kodi a—anthu okwatulidwa amatchedwa chiani, otsalira? Ndi kulondola uko? Chabwino . . . Ine—ine ndikutanthauza ndi—ndi Mkwatibwi. Tsopano, otsalira anasiidwa.

247 Tsopano, pamene mkazi akuti adule pateni ya siketi, inu mumayankhula za izo. Iye amayala nsalu motambasula (ndi kulondola uko?), chidutswa cha nsalu. Ndipo iye amayala pateni yake pansi pa iyo. Iye anayika bwino pomwe pateniyo iti idulidwe. Kulondola?

248 O m'bale, ichi kwenikweni chikuchitirani inu ubwino! Ndani amene anasankha? Mulungu ndiye amasankha! Ndi kulondola

uko? Si za ine kuti ndinenepo, ndi Iye kuti anenepo. Ndipo iye amaika pateniyo pa amene Iye amufuna. Ndi kulondola uko?

249 Tsopano, panali anamwali khumi anatuluka kunja kuti akakomane ndi Mkwati. Ndi kulondola uko?

250 Kodi "namwali" ndi chiani? *Namwali* amatanthauza "wangwiro, woyera." Ndi kulondola uko? Kodi msungwana wa unamwali ndi chiani? Ndi msungwana yemwe sanayambe wakhudzidwapo, iye ndi namwali. Kodi ndi chiani chirichonse chomwe chiri changwiro, monga mafuta aunamwali aazitona? Izo zikutanthauza kuti iwo asungunulidwa mpaka iwo ali mu unamwali wake, iwo ndi angwiro. Kodi golidi waunamwali ndi chiani? Ndi pamene phulusa lonse. . . iye wadutsa motentha ndi chirichonse ndi kubwatitsira kunja phulusa lonse. Nkulondola uko? Zachitsulo zonse ndi galasi, ndi china chirichonse, chabwatitsidwira kunja, iye wangokhala mu unamwali wake.

251 Tsopano, panali khumi anapita kukakomana ndi Mkwati. Yesu ananena choncho. Kulondola uko? Ndi angati akuvomerezana nazo izo, nenani, "Ameni." [Osonkhana ati, "Ameni!"—Mkonzi.] Khumi anapita kuti akakomane ndi Iye. Tsopano, penyani, onse a iwo anali oyera. Chabwino, kuti akhale *woyera* iwo anayenera kuti "anayeretsedwa," chifukwa ndiwo mtsinje woyeretsa wokha umene Mulungu ali nawo, ndiko kuyeretsa. Ndi kulondola uko?

252 Tsopano, penyani. Onse khumi a iwo anali oyeretsedwa, koma asanu analibe Mafuta alionse mu nyali zawo, ndipo asanu anali ndi Mafuta mu nyali zawo. Ndi kulondola uko? Kodi *Mafuta* amaimira chiani? Tsopano, osati ungwiro, unamwali. *Mafuta* amaimira "Mzimu Woyera."

253 Tsopano, ngati ine nditanena ichi kwa. . . ndi kupweteka pang'ono pokha, ine sindikutanthauza izo mu njira yomwe ine ndikuchitira. Tsopano, inu mupirire nane ine, ndipo musati muzijomba ku mpingo. Ine ndiri kokha pa guwa pano kuti ndiyese kukuthandizani inu. Mwaona? Tsopano, penyani, ndiroleni ine ndikuonetseni inu.

254 Palibe mpingo pa dziko lapansi ungakhale moyo mwaungwiro uliwonse kuposa a Nazarene mu ziphunzitso zao, Pilgrim Holiness ndi iwo. Ndi kulondola uko? Iwo mwamtheradi amakhulupirira ungwiro wa kuyeretsedwa, osati. . . ngakhale kwa azimayi awo kumavala mphete, ndi chirichonse. Ungwiro ndi kuyeretsedwa, njira iliyonse, iwo amakhulupirira izo. Mabungwe Achiyero, amwachilamulo onse, icho ndi chiphunzitso chawo, iwo amachikhulupirira icho. Kuyera! Akazi amavala tsitsi lalitali ndi siketi yaitali. Mwamuna sayenera nkomwe kukwinyira mmwamba mikono ya malaya ake, ambiri a iwo. Chirichonse, osati ngakhale kukhudza. . . kusuta, kumwa, chirichonse. . . Osati kanthu ka izo, mwaona. Kuyera! Inu simungakhoze kukhala woyera moposa apo.

255 Koma mpingo womwewo wa Nazarene, ngati munthu akanati ayankhule mu malirime mu mpingo, iye akanati akankhidwire kunja kwa chitseko. Ndipo iwo anati iwo sangakhoze ngakhale kukhala limodzi ndi mmodzi. Tsopano, izo nzoona. Ngati inu simukukhulupirira izo, kayetsereni izo kamodzi, kafufuzeni. Kafufuzeni kamodzi. Iwo amadana ndi maganizo omwe a izo. Iwo amati, "Ndi Mdierekezi!"

256 Asanu a iwo . . . Khumi a iwo anali anamwali. Asanu anali ochenjera amene anali ndi Mafuta mu nyali zawo, ndipo asanu enawo anali angwiro basi ndi oyera koma iwo analibe Mafuta ayi (iwo anali oyeretsedwa, opanda Mzimu Woyera).

257 "Alipo atatu amene amachitira umboni pa dziko lapansi: madzi, magazi, Mzimu." Yohane Woyera 5:7 . . . 1 Yohane 5:7, kani, anati, "Alipo atatu amene amachitira umboni Kumwamba: Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, atatu awa ali Mmodzi. Koma alipo atatu amene amachitira umboni mu dziko lapansi: madzi, magazi, ndi Mzimu, iwo sali chimodzi koma iwo amagwirizana ngati chimodzi."

258 Tsopano, inu simungakhoze kukhala ndi Atate popanda kukhala ndi Mwana. Inu simungakhoze kukhala ndi Mzimu Woyera popanda kukhala ndi Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Iwo ali mmodzi. Inu . . . Iwo ndi osalekanitsika.

259 Koma inu mukhoza kulungamitsidwa popanda kuyeretsedwa. Ndipo inu mukhoza kuyeretsedwa popanda kukhala nao Mzimu Woyera; kumakhala mwachiyero, kumakhala moyo wangwiro, ndi kukhala nawo maonekedwe aumulungu, ndi kumakana Mphamvu ya machiritso ndi kuyankhula mmalirime ndi mphatso zazikulu za Mulungu (ndi chimodzi chirichonse cha izo Mmenemo).

260 Awo ndi anamwali anu asanu ochenjera amene anali ndi Mafuta mu nyali zawo, Chikhulupiriro Chokwatulitsa, kukhulupirira zizindikiro zonse, zodabwitsa, maulosi, ndi chirichonse. Ndipo asanu awa odulidwa kuchokera mwa chotsaliracho anatengedwapo.

261 Ndipo ena onse a iwo anali akanali anamwali ndipo sati adzataike, koma adzapita kupyola nyengo ya Chisautso. Yesu anati "Padzakhala pali . . . "

262 Ndipo iwo anati—iwo anati, "Tipatseniko ife ena a Mafuta anu, ife tikuufuna Mzimu Woyera tsopano."

263 Tsopano, aliyense akudziwa kuti Mzimu Woyera, Zakaria 4, ndi, o, Yakobo 5:14, nonse mukudziwa kuti—kuti amaimira Mzimu Woyera. Tsopano, iwo anati . . . Icho ndi chifukwa chake ife timadzoza ndi mafuta, kuimira Mzimu Woyera; tsopano, "Mafuta a Mzimu," Baibulo limatero.

264 Tsopano, *awa* anali nawo Mzimu Woyera; ndipo *awa* anali oyeretsedwa. *Awa* anali oyeretsedwa kuonjezapo Mzimu

Woyera, akukhulupirira zopambana zonse ndi chirichonse cha Mphamvu ya Mulungu. Chirichonse chimene Mulungu anachiyankhula Umo, iwo anali nacho, amachikhulupirira icho. Awa anatengedwera mmwamba.

265 Ndipo *awa* anati, "Tipatseni ife, kwa ife, tsopano."

266 Anati, "Ife tangokhala ndi okwanira kutitengera ife mkati nao," ndipo kutali iwo anapita mu Mkwatulo.

267 Ndipo iwo anati, "Pitani mukagule kwa iwo amene amagulitsa kwa inu," iwo anatero. Ndipo iwo anapita kuti akayesere kukapemphera mopyola, kuti alandire Mzimu Woyera, koma nyengo ya Amitundu inali itatha ndipo chizunzo chinabuka. Ndipo Iye anati, "Iwo anataidwa mu mdima wakunja komwe kudzakhala kulira ndi kusisima ndi kukukuta kwa mano." Koma mu chiukitsiro chachiwiri iwo adzakhala nkhosa zomwe zidzalekanitsidwe kwa mbuzi, koma osati Mkwatibwi, osati Osankhidwa. Awo ndi otsalira a Mbewu ya mkazi.

268 Chotsalira ndi chiani? Chidutswa chomwe chadulidwa, chitsalira. Nsalu ya mtundu womwewo. Ndi kulondola uko? Inu mukadzidulira diresi yanu ya nsalu, ndipo inu mumatambasula gawo lalikulu la nsalu ndi kuidula iyo. Ndi ntchito yanu pomwe inu muti muyale pateni. Ndi ntchito ya Mulungu pomwe Iye akuti ayale pateni. Iye amamudula iye. Kulondola uko? Ndipo tsopano ichi, chotsalira cha nsalu iyi chimatsalira apa, ndi nsalu yabwino mofanana yomwe ili mu diresi. Nkulondola uko? Koma ndi kusankha kwa Mulungu. Mulungu amausankha Mpingo Wake, Mulungu amaukonzeratu Mpingo Wake; Mulungu anadzozeratu izo, amaudzozeratu Mpingo Wake, ndipo Iye amautengera kunja Mpingo umenewo! Ndipo otsalira amasiidwa kuti adutse mu nyengo ya Chisautso.

269 Ndipo mpamene masikolala ambiri a Baibulo lero afika posokonezeka, kumaganiza kuti Mkwatibwi ali uko mbali iyo mu Chisautso. Wina ananena kwa ine, anati, "Ine sindikanakhoza kukuuzani inu, M'bale Branham." Anati, "Ine ndinamuona Mkwatibwi Kumwamba. Ndipo chinjoka chikumalavula madzi kuchokera mkamwa mwake kuti achite nkhondo ndi Mkwatibwi. Ndipo handiredi ndi forte-foro sauzande, amene ali Mkwatibwi, ataimirira pa Phiri la Sinai."

270 Ine ndinati, "O, ayi. Ayi. Ayi. Ayi. Inu mwachisokoneza icho chonse. Mkwatibwi anali Kumwamba." Ndi *otsalira* a Mbewu ya mkazi, osati iye. . . osati pateniyo, otsalira anali apo, ndipo chizunzo (Ufumu wa Roma) pamene Chikatolika chidzalimbikitsa ndipo iwo adzalumikiza mphamvu zawo pamodzi ndi mpingo Waukulu.

271 Bwanji, iwo ali nacho icho molondola. . . Icho chinali pa televizioni usiku wina. Mpingo wa Methodisti uli kuyesera kulumikiza Amethodisti ndi Abaptisti ndi mipingo yonse yathunthu ya Khristu ikuyesera kulumikizana ndi Chikatolika

ndi kumaima pamaso pa guwa limodzi poyera. Kodi bishopu uja anati chiani pamene iye ankamuzenga mlandu usiku wina uja, kumeneko kuti ndi Mkominisi? Ine ndinali nditaima, ndikuyang'ana pa icho pa televizioni mwiniwanga. Magulu onse a iwo! Ndipo pamene nthawi imeneyo ifika, padzakhala chizunzo chiti chidzauke. Ndiye Mzimu Woyera udzagwa, ndipo Amethodisti, ndi Abaptisti, ndi onsewo, azidzayankhula ndi malirime, kuyamikira Mulungu, ndi kuchiritsa odwala ndi kulosera, ndi zizindikiro zonse ndi zodabwitsa zizidzabwera. Osankhidwa adzapita mmwamba, ndipo otsalawo adzasiyidwa kuno kuti apite kupyola mu nthawi ya Chisautso. Ndipo pakutha pa nthawi, pamene iwo adzaona chomwe chachitika, iwo adzayenera kuti pansi mwa kufera.

272 Ndiye penyani. Inu mukuti, "Chabwino, tsopano, M'bale Branham, kodi inu mukutanthauza kundiuza ine kuti padzakhala . . . awo—anthu awo omwe ati adzakhale uko pa Chiweruzo cha Mpando Woyera?" Iwo adza . . . Mkwatibwi sati adzaweruzidwe konse. Iai, bwana. Iye ali mwa Khristu. Kodi inu mumalowamo bwanji mwa Khristu? "Ndi Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi." Ndi kulondola uko?

273 Tsopano, penyani, penyani apa. Baibulo linati, "Chiweruzo chinaikidwa, ndipo Mabukhu anatsegulidwa." Ndi kulondola uko? Mabuku a ochimwa. "Ndipo Bukhu lina linatsegulidwa," limene liri Bukhu la Moyo, ndipo munthu aliyense anaweruzidwa motero. Ndi kulondola uko? Ndipo ndi ndani yemwe ankachita kuweruzako? Yesu ndi Oyera. Iye anati, "Iye anadza kuti adzatumikire, Nndani Wamasiku Amakezana wathu, Yemwe tsitsi Lake liri longa ubweya." Ndipo anati, "Zikwi khumi kuchulukitsa zikwi khumi anadza limodzi ndi Iye, ndipo anatumikira kwa Iye mu Chiweruzo." Apa Yesu akudza ngati Mfumu ndi Mfumukazi, Ukwati wachitika, ndipo Iye ali wokwatira. Apa pali Mfumu ndi Mfumukazi ataimirira pano. Ndipo apo panaima gulu loyeretsedwa lija, Mulungu anati, "Imirirani kumbali ya kumanja Kwanga apa." Ndilo Bukhu linatsegulidwa, panali ochimwa, "Pitani uko kumanzere Kwanga." Apa ndi iwo amene anali nao maina awo atalembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa.

274 Inu mukuti, "M'bale Branham, dzina langa linalembedwa mmenemo, ine ndidzapita!" Dikirani miniti! Yudasi Isikarioti anayeretsedwa. Fyuu! M'bale, dzuka tsopano, uzitsine, kuti inu muthe kumvetsa Ichi, inu mwaona.

275 Yudasi Iskarioti, mzimu wake ndi wotsutsakhristu lero. Inu mukudziwa zimenezo. Yesu anali Mwana wa Mulungu, anachokera kwa Mulungu ndipo anabwerera kwa Mulungu; Yudasi anali mwana wa chionongeko, anabwera kuchokera ku hade ndipo anabwerera ku hade. Yesu anamtenga wochimwa wolapa limodzi ndi Iye; Yudasi anamtenga wosalapa limodzi

ndi iye, "*Ngati* iwe uli! Ngati! Ngati! Ngati Iwe uli wochiritsa Mwauzimu, chita *ichi*. Ngati iwe uli *Izi*, chita *izi*." (Mwaona, chizindikiro cha funso icho pa Mawu a Mulungu.) "Masiku a zozizwitsa anatha. Ngati Icho chiri, ndisonyezeni ine *izi*. Ngati! Ngati! Ngati!" Mukuona?

"Zonsezo ndi zoona," Mulungu anatero.

276 Tsopano, penyani. Yudasi Iskarioti analungamitsidwa ndi chikhulupiriro, ndipo anakhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu ndipo anabatizidwa. Baibulo linati, "Yesu—Yesu anawabatiza ophunzira, ophunzira Ake." Chabwino.

277 Yohane Woyera 17:17, Iye asanati awatumize iwo kunja, Iye anati, "Ayeretseni iwo Atate, kupyolera mu Choonadi. Mawu Anu ndiwo Choonadi." Ndipo Iye anali Mawu, ngakhale chitetezero chisanachitike. Mwa kuyankhula kwina, "Ngati chionetsero, Atate, ndi Magazi Anga okhetsedwa, Ine ndikuwayeretsa awa."

278 Iye anawapatsa iwo mphamvu yotsutsira mizimu yosayera, ndipo iyo inkatuluka ndipo iwo ankatulutsa ziwanda. Ndi kulondola uko? Ndipo iwo anachiritsa odwala. Ndi kulondola uko? Ndipo iwo anabwerera, oyeretsedwa, akusangalala, akulumphalumpha, akufuula, ndi kumayamika Mulungu. Ndi kulondola uko? Ndipo anati, "Ngakhale ziwanda zikutimvera ife."

279 Ndipo Yesu anati, "Musati inu muzisangalala chifukwa ziwanda zikukumverani inu, koma zisangalalani chifukwa maina anu analembedwa mu Bukhu la Kumwamba." Ndi kulondola uko? Ndipo Yudasi Iskarioti anali ndi iwo, mmodzi wa iwo, wotulutsidwa, woyeretsedwa, ndipo dzina lake litalembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Werengani Mateyu 10 ndipo muone ngati uko si kulondola. Iye anamuitana mmodzi aliyense wa iwo, ndipo Yudasi ndi mmodzi aliyense wa iwo, anali uko komwe. Iye anawatumiza iwo kunja, nkuwapatsa iwo mphamvu yotsutsa mizimu yoipa.

280 Tsopano penyani! Valani chovala chanu chosalowa nyese. Koma pamene Yudasi anadza mu mpingo womwewo uko, monga msungichuma wa mpingo, akugwira ntchito ndi m'busa . . . Yesu. Koma pamene izo zinafika ku nthawi ya Pentekoste, iye anasonyeza maanga ake. Iye anasonyeza chomwe iye anali. Ndipo ndi—ndi khalidwe lokwanira pa iye, iye anadziwononga yekha ndi kudzipachika yekha pa mtengo wa mkuyu, kuti akwaniritse uneneri. Ndipo mzimu uja wa Yudasi udzatulukira apo ndi kumakhulupirira Ambuye Yesu Khristu. Monga Yesu anati, "Ziwanda zimakhulupirira ndipo zimanthunthumira." Iye adzadza apo pomwe ndi kudzaphunzitsa chiyeretso, mwangwiro basi monga moyo woyera ungakhalire; koma pamene izo zidza ku ubatizo wa Mzimu Woyera ndi mphatso za Mzimu, iye

adzazikana Izo! Iye amasonyeza maanga ake nthawi zonse. Ndi umenewo mzimuwo mo—. . .

281 Ndipo Yesu anati, "Chenjerani!" Mateyu 24, kachiwiri. "Mizimu iwiriyo idzakhala yoyandikana kwambiri mpaka iyo idzanyenga Osankhidwa omwe. . . " Ndi kulondola uko? Pamene pateni iyo yayalidwa. . . M'bale, kuli bwino inu mukhulupirire mwa alaliki akachitidwe-kachikale, a Mzimu Woyera komwe kuno ndi kukhala moyenera ndi Mulungu. Ndiko kulondola. Musati mukhale ndi maonekedwe aumulungu ndi kumakana Mphamvu yakeyo. Ameni! Aliyense akumverera bwino? [Osonkhana ati, "Ameni!"—Mkonzi.]

Mmene tifika Kumwamba,
Lidzakhala tsiku lachimwemwe!
Tikadzamuona Yesu,
Tidzaimba ndi kufuula chigonjetso.
Mmene tifika Kumwamba,
Lidzakhala tsiku lachimwemwe!
Tikadzamuona Yesu,
Tidzaimba ndi kufuula chigonjetso.

282 Aleluya! Tiyeni tiime kamphindi kokha. Ndi angati akumukonda Iye ndi mtima wanu wonse? Kwezani mmwamba manja anu, itini "Ambuye alemekezeke!" [Osonkhana ati, "Ambuye alemekezeke!"—Mkonzi.] "Ambuye, ine ndikukhulupirira Uthenga wonse." [Osonkhana ati, "Ambuye, ine ndikukhulupirira Uthenga wonse."—Mkonzi.] "Mundithandize ine kuti ndikhale wantchito Wanu." [Osonkahana ati, "Mundithandize ine kuti ndikhale wantchito Wanu."—Mkonzi.] Aleluya! Aleluya! Kodi inu mukumukonda Iye? [Osonkhana ati, "Ameni!"—Mkonzi.] Mu Baibulo iwo. . .

283 Mkazi wina anati kwa ine mmodzi. . . mnyamata, iye akhoza kukhala akumvetsera usikuuno, iye amakhala kudutsa mseuwu basi. Iye anabwera kumeneko. Ndipo Mlongo Lula amene ankakonda kubwera kuno ku mpingo, iye anali kumafuula kumbuyo uko. Ine ndinali kulalikira, M'bale Neville. Ndipo mnyamata uyo anati kwa ine. . . Tsopano, iye anali mphunzitsi wa Sande sukulu kumunsi uko ku mpingo wa First Baptist. Iye anati, "Billy, ine ndinali kukomedwa ndi ulaliki wanu mpaka mkazi uja atayamba kulira ndi kufuula, 'Zikomo Inu, Yesu! Alemekezeke Ambuye!' Ndipo kamodzi pa kanthawi" anati "mwamuna wina anati," (M'bale Seward) "anafuula, 'Ambuye alemekezeke! Ameni!'" Ndipo ine ndinali ndikulalikira pa *Kutaya Maufuluakubadwa Ako*, Esau anagulitsa Ufuluwakubadwa wake. Ndipo ine ndinali kupitirira, ndipo iwo anali kumangofuula, kumapitirira. Ndipo anati, "Uuuu," anati, "izo—izo zimangopangitsa zanzi kudutsa pa msana wanga." Anati, "Ine sindikanakhoza kuzipirira izo!"

284 Ine ndinati, “M’bale, ngati inu muti mudzakafike Kumwamba inu mukanati mukakongwe ngati mufe.” Ine ndinati, “Uko zedi kuli kufuula Kumwamba, usana ndi usiku.” Ndipo uko nkulondola, m’bale. O, inde, bwana!

O, ndifuna kumuona, pa nkhope Yake,
Kukaimba za chisomo Chake;
Pa misewu ya Ulemerero ndzakweza liwu langa;
Zonse zatha, ndiri kwathu, mosangalalabe.

O, ndifuna kumuona, pa nkhope Yake,
Kukaimba za chisomo Chake;
Pa misewu ya Ulemerero ndzakweza liwu langa;
Zonse zatha, ndiri kwathu, mosangalalabe.

285 Ameni! Chabwino, M’bale Neville. Mulungu akudalitseni inu. Fikani apo pomwe ndi kukatseka.

Khalidwe Dongosolo ndi Chiphunzitso cha Mpingo, Bukhu Loyamba
(Conduct, Order And Doctrine Of The Church, Volume One)

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham olalikidwa ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Ndipo kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org